# Buku la Mphunzitsi

## Nthawiyabaibulo
## Kalasi 0, Yoyamba ndi Yachiwiri

### Maphunziro B7 - B12

www.besweb.com

## Bible Educational Services

Registered Charity UK (No 1186004)

**Cholinga cha Utumiki**
Kukonzera ena maphunziro a Baibulo kuti apereke choonadi cha Yesu ku m'bado otsatira pa dziko lonse lapansi.

**Masomphenya a Utumiki**
Kupereka ku m'bado wotsatira maphunziro okwanira, m'chiyankhulo chawo powalembera ndi kuwathandiza komanso kuthandiza anzathu ena onse odzipereka pa dziko lonse.

## ZOYENERA KUDZIWA

**Zomwe a Bible Educational Services amachita**
A Bible Educational Services (BES UK) amasindikiza maphunziro a "Nthawiyabaibulo", "Moyo Watsopano" ndi "Okolola" a m'Chingerezi komanso amathandiza a Postal Bible Schools ndi mabungwe ena amene amagwiritsa ntchito maphunziro a BES ku UK ndi ku mayiko a kutsidya la nyanja pokawachezera, kugwira nawo ntchito limodzi, kuwalangiza ndi kuwaphunzitsa. BES imagwiranso ntchito pamodzi ndi magulu ena amene akugwira ntchito yomasulira maphunzirowa m'ziyankhulo zawo, pomasulira, kusindikiza ndi kupereka maphunziro kwa anthu ena. Maphunzirowa amaperekedwa mwaulere kwa ophunzira onse.

Maphunziro a Nthawiyabaibulo anayamba kugwiritsidwa ntchito ku Kumpoto kwa Ireland zake 60 zapitazo. A Bible Educational Services ndi amene ali ndi udindo woyang'anira ntchito yosindikiza maphunzirowa m'Chingerezi ndi m'ziyankhulo zina zonse. Maphunziro a Nthawiyabaibulo amasindikizidwa mu A4 ndipo amathandiza ophunzira m'madera ena kuti masabata anayi aliwonse azitha kutumiza mayankho ku Postal Bible School Centre kuti akachonge. Posachedwapa, tikuyamika a bungwe la Every Home Crusade (Bungwe la Chitsistimutso) ku Belfast, anayamba kusindikiza maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi amene amatchedwa A5. Amenewa amagwiritsidwa ntchito m'matchalichi ndi m'sukulu makamaka ku mayiko akunja kuti akhale osavuta chifukwa kumeneko njira zotumizira ndi zovuta kwambiri.

Maphunziro a BES ndi apadera kwambiri chifukwa amatha kugwiritsidwa ntchito m'nyumba kapena pa gulu (tchalichi kapena sukulu), potsatira ndondomeko imene imalola ophunzira kuphunzira kwa zaka makumi awiri. Gulu lililonse lili ndi maphunziro asanu molingana ndi zaka zawo, Amene sanayambe sukulu (Kalasi 0), zaka 5-7 (Kalasi Yoyamba), zaka 8-10 (Kalasi Yachiwiri), zaka 11-13 (Kalasi Yachitatu), zaka 14-16 (Kalasi Yachinayi). Pali ndondomeko ya kaphunzitsidwe ya zaka zitatu ya gulu lililonse molingana ndi zaka zawo. (Onani peji 4.) Magulu angathe kusintha molingana ndi kuthekera kwawo. A Bibletime Resource amapereka mpata kwa ana kuphunzira Mawu a Mulungu ndi kutha kuzindikira kufunika kwa Uthenga Wabwino pa miyoyo.

Maphunziro akupezeka m'Chingerezi pa BES website – www.besweb.com kapena kuchokera kwa Mlembi Wamkulu. Amapezekanso pa website ya ziyankhulo zina. BES ali ndi zomwe analemba zothandiza amene akufuna kugwira nawo ntchitoyi, ndipo zimenezi zilinso pa website yawo.

## Keyala

**International and Northern Ireland Secretary (stockist of all English lessons)**
Mr S Balmer, BES Office (UK), 37a Belmore Street, Enniskillen, Northern Ireland. BT74 6AA
Phone: 00 44 286 632 2462
Email: sam@besweb.com

**UK Secretary – Editorial feedback**
Mr Stephen Gillham
Email: stephen.gillham@besweb.com

**Web address:** www.besweb.com
**Email address:** info@besweb.com

## BUKU LA MPHUNZITSI

Poyamba, maphunziro awa anakonzedwa ndi cholinga choti akhale otumizira anthu, koma lero maphunzirowa akugwiritsidwa ntchito kwambiri pamene njira zotumizira ndi zosadalirika. M'madera ena monga ku mipingo ya ku Afrika, India ndi mayiko ena kulibe njira zotumizira zodalirika. Chifukwa cha ichi, Buku la Mphunzitsi linakonzedwa kuti lithandize amene sangathe kulandira pa positi. Buku la Mphunzitsi m'buku lino ndi la Kalasi 0, Yoyamba ndi Yachiwiri.

Buku la Mphunzitsi lililonse lili ndi ndime zonse zimene zili m'maphunziro a Nthawiyabaibulo. Maphunziro a Nthawiyabaibulo ndi Buku la Mphunzitsi zinakonzedwa kuti zigwire ntchito sabata lililonse. Maphunziro a mwezi wa Epulo amafotokoza za Paska ndipo a mwezi wa Disembala za Khirisimasi.

Madera ena amagwiritsa ntchito maphunziro a pa mwezi otchedwa A4, amene ali ndi maphunziro anayi ndipo ena amagwiritsa ntchito maphunziro otchedwa A5 amene ali ndi maphunziro 24. Mphunzitsi kapena mtsogoleri akuyenera kupereka maphunziro a A4, ndipo sabata lililonse azilemba mayankho a phunzirolo m'tchalichi, ku sukulu kapena ku nyumba ndi kupereka mayankhowo sabata lotsatiralo. Kumapeto kwa mwezi, mphunzitsi kapena mtsogoleri adzilandira maphunzirowo ndi kukachonga, akatsiriza abwere nawo ndi kupereka kwa ophunzirawo.

Ngati ophunzira akugwiritsa ntchito buku, mphunzitsi atenge bukulo kumapeto kwa phunziro lililonse ndi kukachonga. Koma tikudziwa kuti madera ena izi ndi zosatheka. Ngati akuphunzira m'kalasi, ophunzira asinthane mabuku awo ndipo mphunzitsi kapena mtsogoleri awathandize kupeza mayankho ndipo ophunzirawo achongelane maphunziro awo. Kumapeto kwa bukuli kuli malo oyika marikisi amene wophunzira wapeza mwezi uliwonse ndiponso malo a ndemanga ya mtsogoleri ya momwe wophunzirayo akuchitira m'kalasi. Palinso satifiketi yomwe wophunzira ayenera kulandira yoonetsa marikisi ake a maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi.

Timakondwera pamene anthu akutifotokozera zomwe akukumana nazo pogwiritsa ntchito Buku la Mphunzitsi ndi mabuku a Nthawiyabaibulo ndipo tumizani ndemangazo kwa stephen.gillham@besweb.com.

## KUKONZEKERA KWA APHUNZITSI

Buku la Mphunzitsi si lotsekeka kuti mphunzitsi sangathenso kuyikapo zinthu zina zomwe akuziona kuti ndi zothandiza pophunzitsa. Nawa malangizo othandiza pogwiritsa ntchito Nthawiyabaibulo.

- **Kudziwa bwino nkhani** - Aphunzitsi akuyenera kudziwa bwino nkhani ya m'Baibulo komanso phunziro la Nthawiyabaibulo lomwe akugwiritsa ntchito. Nkhani ndi yakuti, mphunzitsi awerenge phunzirolo nthawi yophunzitsa isanakwane. Iye amvetse bwino ndondomeko ya phunziro lililonse kuti akonzekere bwino kuphunzitsako.
- **Kumvetsa phunziro lokaphunzitsa** - Poyamba pa ndondomeko ya phunziro lililonse pali mawu akuti, "Ife tikuphunzira kuti" motsatidwa ndi zolinga ziwiri zophunzirira zomwe mwina ana angamvetse ngati mphunzitsi atafotokoza, kenaka pali gawo lotsiriza phunziro la Nthawiyabaibulo. Cholinga chophunzirira ndi kufuna kudziwa nkhaniyo, pamene chachiwiri ndi cholimbikitsa ophunzira kuti aganizire zomwe aphunzirazo ndi kuzigwiritsa ntchito pa moyo wawo. Zolinga zimenezi zikugwirizana kwambiri ndi fundo/choonadi cha m'phunzirolo ndipo aphunzitsi akuyenera kugwiritsa ntchito zimenezi kuti adziwe momwe aphunzitsira ndi zomwe ana aphunzira.
- **Mawu oyamba** - Maphunziro onse akuyamba ndi mawu akuti, "kumene kuli ana" ali ndi zomwe akukumana nazo. Pali njira zambiri zomwe tapereka zothandiza ana kutenga mbali pa zokambirana nthawi ya maphunzirowo.
- **Kuphunzitsa** - Fundo zazikulu za phunziro tapereka. Tikuyembekezera kuti aphunzitsi sadzikhalanso akumaziwerenga pamene akuphunzitsa koma kuti akhala atadziwa bwino nkhani yonse ndipo adzitha kufotokoza nkhaniyo mochititsa chidwi. Mphunzitsi ayesetse kuti ana amvetse mitu ya maphunzirowo kuchokera pa nkhani yomwe akuphunzira ndiponso awathandize kumvetsetsa zoyenera kuchita kuchokera mu nkhaniyo. Pamene m'poyenera tayesetsa kufotokozera bwino monga nkhani chabe. Mawu amenewa tawalemba motere: ***ITALICS***.
- **Kuphunzira** - Nkhani iliyonse ili ndi Vesi Yoloweza. Malo ena muli Mavesi Oloweza awiri; taonjezera vesi ina yomwe tikuona kuti itha kukhala yothandiza kuti ana aphunzire mosavuta. Tikukhulupirira kuti ana adzaphunzira Mavesi Oloweza ndipo aziwakumbukira kotero kuti adzadziwa mavesi ambiri.

- **Kutsiriza** - Kwa amene akuphunzira m'kalasi, mphunzitsi ayenera kudziwa ngati ophunzira angathe kutsiriza ntchito yawo ndiponso za thandizo lomwe likufunika kuchokera kwa mphunzitsiyo. Kwa ophunzira ena padzafunika kuti mphunzitsi aziwerenga nkhaniyo, ophunzirawo n'kumatsatira kapena kumvera. Koma enanso adzatha kuwerenga okha nkhaniyo. M'njira zonse ziwiri, ndi kofunika kuwauza malangizo okhudzana ndi mafunso. Ngati Nthawiyabaibulo sikuchitikira m'kalasi, n'kofunika kuti aphunzitsi azipezeka kuti azithandiza kuyankha mafunso osati aziyankha ngati a m'kalasi wamba. Ophunzira ayenera kumasangalala, kulimbikitsidwa ndi kuyamikiridwa pamene kuphunzira.
- **Kukumbutsana** - Zomwe zingatheke chitani, khalani ndi nthawi ya mafunso, ya masewero ndi zina zambiri. Izi zidzathandiza kuphunzira ndi kukumbukira pamtima nkhaniyo.
- **Kuonetsa** - Nthawi zina, zinthu zoti muonetse zidzakhala zovuta kuzipeza koma ngati n'kotheka yesetsani kupeza zithunzi kapena zida zina zothandiza kuti ophunzira amvetse nkhaniyo. Zinthu zimene ophunzira akuziona zimathandiza kwambiri pofotokoza nkhani. Pamene n'zotheka, pezani zithunzi kuchokera ku www.freebibleimages.org (FBI) zomwe mungathe kulandira. Kumapeto kwa Buku la Mphunzitsi kuli zina zoonjezera momwe akufotokoza kwina kumene mungapeze zithunzi za nkhani za m'Baibulo mwaulere.
- Ngati mungapeze fotokope mutha kukulitsa zithunzizo, kukhala za kalala ndi kuzigwiritsa ntchito pophunzitsa.

## Nthawi ya Phunziro

- **Machitidwe.** M'buku la Mphunzitsi muli machitidwe a phunziro lililonse, koma mphunzitsi ali ndi ufulu nthawi ndi nthawi kusintha machitidwe ake.

1. Mawu Oyamba ndi kufotokoza nkhani - mphindi 15
2. Kuphunzitsa Vesi Yoloweza – mphindi 5 mpaka 10
3. Kutsiriza kulemba - mphindi 20
4. Mafunso ndi zochitika zina mpindi 5 mpaka 10.

Kumbukirani mawu ofunika awa:

"Ndiuzeni ndipo ndidzayiwala,
ndionetseni ndipo ndidzakumbukira,
loleni ndichite nawo ndipo ndidzamvetsetsa."

## Zophunzitsa Nthawiyabaibulo

| | KALASI 0 (sanayambe sukulu)<br>Kalasi Yoyamba (Zaka 5-7)<br>Kalasi Yachiwiri (Zaka 8-10) | Kalasi Yachitatu<br>(Zaka 11-13) | Kalasi Yachinayi<br>(Zaka 14+) |
|---|---|---|---|
| MAPHUNZIRO A | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Abrahamu<br>6. Abrahamu<br>7. Petro<br>8. Petro<br>9. Yakobo<br>10. Akhristu Oyambirira<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Pemphero<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe ndi Kugwa<br>2. Zochitika Zoyamba - Genesis<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Moyo wa Chikhristu<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO B | 1. Moyo Woyambirira wa Khristu<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Mafanizo<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Alembi a Uthenga Wabwino<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yakobo ndi Banja Lake<br>7. Yosefe<br>8. Machitidwe 2:42 - Zoyenera Kuchita<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Lamulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO C | 1. Danieli<br>2. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>3. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute ndi Samueli<br>6. Davide<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Yona<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>3. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Amene Mulungu Anawagwiritsa Ntchito - Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Zoyankhula za Yesu<br>3. Mphamvu za Ambuye<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Ena a mu Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |

## B7 Nkhani Yoyamba

**Kufika kwa abale a Yosefe – Iyi ndi nkhani ya zotsatira za zolakwa zimene timachita.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Maloto a Yosefe okhudza abale ake anakwaniritsidwa.<br>• Zinthu zoyipa zomwe timachita zidzatibwerera m’tsogolo.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Agalatiya 6: 7***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Genesis 42: 1-26*** |
| **MAWU OYAMBA** | Ana akambirane awiriawiri nkhani ya Yosefe pamene yafika. Pezani zinthu zoyipa ndi zabwino zomwe zachitika mpaka pano. Tsirizani ponena kuti zinthu zakhala zikuchitika mokomera Yosefe ngakhale abale ake anamuzunza. Nanga abale ake abwerera bwanji ku dziko la Kanani? Nkhani ya lero ikutitengeranso ku Kanani. |
| **PHUNZITSANI** | • Kwawo ku Kanani anthu anali ndi njala. Kunali chilala ndipo anthu analibe chakudya choti angadye. Yakobo anamva kuti ku Aigupto kunali chakudya chambiri. Iye anawuza abale a Yosefe kuti apite ku Aigupto kukagula chakudya cha banja lawo. Abale onse anapita kupatula mng’ono wake wa Yosefe, Benjamini. Funsani ana apeze chifukwa chomwe iye sanapite nawo. ***(Genesis 42: 1-5)***<br>• Ku Aigupto, Yosefe ndiye anali wamkulu wokayang’anira zogulitsa chakudya. Pamene abale anafika, onse anabwera ndi kugwada pamaso pa Yosefe, Bwanamkubwa wa Aigupto! ***(Genesis 42: 6-7)***<br>• *Kumbutsani ana maloto amene Yosefe analota za abale ake asanamugulitse. Kambiranani za kukwaniritsidwa kwa maloto akewo.*<br>• Yosefe anachita ngati sanawadziwe abale akewo ndiponso iwo sanamuzindikire. Iye anawayankhula ngati anali alendo ndipo anati, “Ndinu azondi! Mwabwera kudzazonda dziko lathu!” Abale ake anamuwuza kuti zimenezo sizinali zoona. Iwo anamuwuza Yosefe kuti anali anthu owona mtima, ana a munthu m’modzi. Iwo anamuwuza Yosefe kuti anali ndi m’bale wawo amene ‘palibe’ ndipo wamng’ono anali ku mudzi kwawo. Pofuna kuwayesa kuti adziwe ngati akunena zoona, Yosefe anawawuza kuti abwerere kwawo ku Kanani ndi kukatenga mng’ono wawo. Pofuna kuonetsa kuti adzabweranso, anasunga m’bale wawo m’modzi, Simeoni, m’ndende. ***(Genesis 42: 8-20)***<br>• Funsani ana momwe abalewo ankamvera m’mitima mwawo. Iwo anakambirana pakati pawo zomwe zinkawachitikira. Iwo anazindikira kuti anachita zoyipa kwa Yosefe zaka zam’mbuyomo. *Fotokozani kuti tsopano azindikira kulakwa kwawo ndipo zotsatira za tchimo lawo zawapeza. Onani pa* ***Numeri 32: 23*** *pamene akuti, “Zindikirani kuti tchimo lanu lidzakupezani.”*<br>• Iwo anali ndi chitsimikizo kuti Mulungu ankawalanga chifukwa cha zomwe anachita kwa Yosefe. Yosefe ankamva zonse zimene ankayankhula. Iye anapita kumbali ndi kukalira. ***(Genesis 42: 21-24)***<br>• Yosefe analamulira anthu ake adzaze tirigu m’matumba a abale ake. Iye analamulanso kuti ayike ndalama zawo m’matumbamo ndi kuwapatsa chakudya cha pa ulendo. Abalewo ananyamula pa abulu awo ndi kuchoka ku Aigupto kubwerera kwa abambo awo. ***(Genesis 42: 25-26)***<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI mu Zoonjezera A – Kufika kwa abale a Yosefe. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n’koyenera Vesi Yoloweza: ***Agalatiya 6: 7***. Kumbutsani ana kuti tchimo nthawi zonse limatibweretsera mavuto. Baibulo limati zili ngati kufesa mbewu ndipo kenaka tsiku lina zimamera ndi kukhala chomwe tinafesa chija. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.<br>• N’chifukwa chiyani abale ake anabwera ku Aigupto?<br>• Kodi ndi ndani amene ankagulitsa tirigu ku Aigupto?<br>• Kodi abale a Yosefe anamuzindikira?<br>• Kodi Yosefe anati abale akewo anali ndani?<br>• Kodi Yosefe anafuna kuti abale akewo adzabwere ndi chiyani ku Aigupto?<br>• Kodi ndi m’bale uti amene anayikidwa m’ndende?<br>• Kodi abale ake ankaganiza kuti izi zikuwachitikira chifukwa chiyani? |

## B7 Nkhani Yachiwiri

**Benjamini ndi nkhani yoyipa – Iyi ndi nkhani ya momwe zochita zathu zimakhudzira ena.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yosefe ankakondabe abale ake ngakhale iwo anamuchitira zoyipa.<br>• Mulungu amatikonda ngakhale ife takhala tikuchita zolakwa.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Aefeso 4: 32***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Genesis 42: 26 - 44: 13*** |
| **MAWU OYAMBA** | Uzani ana aganizire kuti iwo ndi m'modzi mwa abale a Yosefe amene akuchoka ku Aigupto kubwerera kwawo ku Kanani. Muli ndi chakudya chokwanira kudyetsa banja lanu lonse tsopano! Kodi akumva bwanji m'mitima mwawo? Tsopano taganizani atangotsekula matumba awo sakupezamo tirigu yekha komanso ndalama zomwe anagulira tiriguyo! Kodi wayika m'menemo ndi ndani? Kodi ndi msampha? Kodi Bwanamkubwa wa Aigupto aganiza kuti aba? Kodi mungapitenso bwanji ku Aigupto kukagula chakudya china?<br><br>Njira ina, pezani zinthu monga thumba, chakudya ndi ndalama ndi kuchita sewero ndi ana. |
| **PHUNZITSANI** | • Izi ndi zomwe zinachitika kwa abale onse pamene ankabwerera kwawo. Thandizani ana kuti aganizire momwe abale ankamvera m'mitima mwawo. ***(Genesis 42: 26-28)***<br>• *Funsani ana kuti ndi chifukwa chiyani akuganiza kuti Yosefe ndi amene anayika ndalamazo m'matumba awo. Kumbutsani ana kuti abale anazindikira kuti izi zikuchitika chifukwa cha zoyipa zomwe anachitira Yosefe.*<br>• Atafika kwawo, iwo anawuza abambo awo zomwe zinachitika. Iwo anafotokozera abambo awo kuti Bwanamkubwa wa ku Aigupto ananena kuti iwo anali azondi. Iye ankafuna kuti apite ndi Benjamini. Yakobo atamva izi ndi kuona ndalama zawo zili m'matumba awo, iye anachita mantha. ***(Genesis 42: 29-38)*** *Kodi mukuganiza kuti Yakobo alola kuti Benjamini apite nawo ku Aigupto?*<br>• Masiku akupita, njala inakula kwambiri. Banja la Yakobo linabenso chakudya. *Thandizani ana kuti amvetsetse vuto la Yakobo nthawi imeneyi.* Iye anawuza abale aja kuti apitenso ku Aigupto kukagula chakudya. Yuda anawuza abambo ake kuti sakanatha kupitanso popanda Benjamini. Iye anadzipereka kukaonetsetsa kuti Benjamini ali bwino. Palibe chimene Yakobo akanachita. Iwo ankafuna chakudya. Iye anavomereza kulola Benjamini kuti apite ku Aigupto. Iye anawuza abalewo kuti atenge ndalama zija ndiponso mphatso zoti akapereke kwa Bwanamkubwa. ***(Genesis 43: 1-14)*** *Kodi mukuganiza kuti abalewo ankamva chiyani m'mitima mwawo pamene ankapita ku Aigupto kukakumana ndi Bwanamkubwa wa ku Aigupto?*<br>• Abale anafika ku Aigupto ndipo anayima pamaso pa Yosefe. Yosefe ataona Benjamini pakati pawo, anawuza antchito ake kuti awakonzere phwando lalikulu m'nyumba mwake. Iye analamulira kuti atulutse Simeoni ku ndende. Yosefe atafika pa phwandopo abale ake anamugwadiranso. Kumbukirani maloto a Yosefe. Iye anawafunsa za moyo wa abambo awo ndiponso anayankhula ndi Benjamini. Yosefe anakhudzika mu mtima ndipo anatuluka m'chipindamo. *Posatengera zonse zimene zinamuchitikira, iye ankakonda abale ake. Makamaka Benjamini amene anali mng'ono wake wa mayi m'modzi.* Pamene Yosefe anabweranso, anapereka chakudya ndipo onse anadya pamodzi. ***(Genesis 43: 15-34)*** *Fotokozani kuti ngakhale tachita zolakwa, Mulungu amatikondabe.*<br>• Tsiku lotsatira m'mawa abale aja ananyamuka kukapita ku Kanani atadzaza matumba awo ndi tirigu. Nthawi iyi Yosefe anayika kapu yake yapadera yasiliva m'thumba la Benjamini. Yosefe anatumiza antchito ake kuti afufuze za kapuyo. Kapu inapezeka m'thumba la Benjamini! Iwo anabwereranso ku Aigupto! ***(Genesis 44:1-13)*** *Kodi iwo tsopano akumva chiyani m'mitima mwawo? Kodi ana angathe kuganiza zomwe zichitike kenaka?*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Benjamini ndi nkhani yoyipa. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Aefeso 4: 32***. Kambiranani mawu akuti 'kukhululuka'. Fotokozerani ana kuti Mulungu amatikonda ndipo ndi wokonzeka kutikhululukira pamene tavomereza zoyipa zomwe tachita. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.<br>• Kodi abalewo anapeza chiyani m'matumba mwawo?<br>• Kodi Yakobo ankafuna kuti Benjamini apite ku Aigupto? Ngati si choncho, chifukwa chiyani?<br>• Ndani anadzipereka kusamalira Benjamini?<br>• Kodi Yosefe anamva bwanji mu mtima mwake pamene anaona Benjamini?<br>• Kodi Yosefe ankakondabe abale ake?<br>• Kodi kapu inapezeka m'thumba la ndani?<br>• Kodi kukhululuka zikutanthauza chiyani?<br>• Kodi ife timafuna kuti Mulungu atikhululukire? Chifukwa chiyani? |

## B7 Nkhani Yachitatu

**Kukhululuka ndi nkhani yabwino – Iyi ndi nkhani ya momwe tikuyenera kukhululukirana.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yosefe anakhululukira abale ake pa zomwe anamuchitira.<br>• Mulungu amakonda aliyense wa ife ndipo akufuna atikhululukire zoyipa zomwe timachita.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Genesis 45: 8***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Genesis 44: 14 - 45: 28*** |
| **MAWU OYAMBA** | Kumbutsani ana kuti abale a Yosefe afika ku Aigupto mpaka pamene yafika. Kapu yasiliva, yomwe inali ya Yosefe, inapezeka m'thumba mwa Benjamini. Abale anabwerera ku Aigupto ali ndi chisoni chachikulu. Kodi Bwanamkubwa akachita chiyani? Kodi Benjamini akaphedwa kapena kutsala kuti akhale kapolo? Kodi chidzachitika ndi chiyani kwa abambo awo iwo akabwerera ku Kanani opanda Benjamini? |
| **PHUNZITSANI** | • Abale aja anafika m'nyumba ya Yosefe. Iye anaoneka ngati wakwiya kwambiri chifukwa chotenga kapu yake yasiliva. Yuda anayankhula. Iye anazindikira kuti zoyipa izi zinawachitikira chifukwa iwo anali olakwa. *Fotokozani 'kulakwa' kwawo.* Abale a Yosefe onse anadzipereka kuti akhale akapolo ake. Koma Yosefe anati ndi munthu yekhayo amene anapezeka ndi kapu yake m'thumba mwake ndiye akhale kapolo wake. Benjamini ankayenera kutsala! ***(Genesis 44: 14-17)***<br>• Yuda anayankhulanso. Iye anawuza Yosefe kuti ngati Benjamini sabwerera kwawo, abambo ake akafa ndi chisoni chachikulu. Yuda anadzipereka kuti atsale m'malo mwa Benjamini. ***(Genesis 44: 18-34)*** *Kambiranani za kusinthika kwa mitima ya abalewa. M'bale amene anawuza ena kuti agulitse Yosefe ku ukapolo ndi amene akudzipereka kuti akhale kapolo! Yosefe anatha kuona kuti abale ake tsopano akukondana ndiponso akukonda abambo awo.*<br>• Yosefe anadziwa kuti nthawi yakwana yoti awuze abale ake za kuti iye anali yani. Anawuza aliyense kupatula abale ake kuti atuluke m'chipindamo ndipo kenaka anati, 'Ine ndine Yosefe.' *Kambiranani zomwe abale ankamva m'mitima mwawo tsopano.* Kodi Yosefe afuna kuti abwezere zomwe anamuchitira? M'malo mwake, Yosefe anawatsimikizira kuti ichi chinali chikonzero cha Mulungu kuchokera pachiyambi. Mulungu anatumiza Yosefe ku Aigupto kuti adzapulumutse miyoyo yawo nthawi ya njala. ***(Genesis 45: 1-8)***<br>• *Kambiranani nkhani ya kuti Yosefe anakhululukira abale ake. Mulungu adzatikhululukira zoyipa zomwe timachita ngati tingalape. Monga Yuda mu nkhaniyi, tikuyenera kuzindikira ndi kuvomereza kuti tachita zinthu zambiri zolakwa m'miyoyo yathu.*<br>• Yosefe anadziwa kuti patsala zaka zisanu kuti njala ithe. Iye ankafuna kuti banja lake likhale pabwino. Iye anawuza abale ake kuti abwerere kwawo ndi kukafotokozera abambo awo zomwe zachitika. Kenaka akanyamule katundu wawo ndi kubwera kudzakhala ku Aigupto. ***(Genesis: 45: 9-28)***<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kukhululuka ndi nkhani yabwino. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Genesis 45: 8***. (Gwiritsani ntchito gawo loyamba la vesi.) Kumbutsani ana kuti zonse zimene zinachitika pa moyo wa Yosefe chinali chikonzero cha Mulungu chofuna kupulumutsa banja la Yakobo mu nthawi ya njala. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.<br>• Kodi m'thumba la Benjamini anapezamo chiyani?<br>• Kodi ndi ndani amene Yosefe ankafuna kuti atsale ndi kukhala kapolo wake?<br>• Kodi ndi ndani anadzipereka kuti alowe m'malo mwa Benjamini?<br>• Kodi chikanachitika ndi chiyani ndi Yakobo ngati Benjamini akanapanda kubwerera kwawo?<br>• Kodi Yosefe anadziwa bwanji kuti mitima ya abale ake inasintha?<br>• Kodi Yosefe anakhululukira abale ake?<br>• Kodi tichite chiyani kuti Mulungu atikhululukire machimo athu? |

## B7 Nkhani Yachinayi

**Onse pamodzi mu Aigupto – Iyi ndi nkhani ya chikonzero cha Mulungu pa Yosefe.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yosefe anakumananso ndi abambo ake Yakobo.<br>• Mulungu amatha kubweretsa zabwino mu nyengo zovuta ngati tingamudalire kwathunthu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Genesis 50: 20***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Genesis 46: 1-34*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za kuyanjananso ndi kukumana ndi munthu amene munasiyana kalekale. Kodi izi zinachitikapo m'banja mwanu? Nthawi zina anthu amasangalala mpaka kukhetsa misozi ya chimwemwe! Mu nkhani yathu lero timva za kuyanjananso kopatsa chidwi. |
| **PHUNZITSANI** | • Yakobo (Israyeli) ndi banja lake anasokhanitsa pamodzi katundu wawo. Anasonkhanitsa ziweto zawo ndi kuyamba ulendo wopita ku Aigupto. Ali pa ulendo opita ku Aigupto anayima pa malo otchedwa Beereseba ndi kupereka nsembe kwa Mulungu. *Fotokozani kuti ankathokoza chifukwa Mulungu ankawasamalira bwino!* ***(Genesis 46: 1)***<br>• Mulungu anayankhula ndi Yakobo m'maloto. Iye anawuza Yakobo kuti asachite mantha kupita kukakhala ku Aigupto. Ku Aigupto, Mulungu akadalitsa Yakobo ndi kukulitsa banja lake kukhala mtundu waukulu. Iye analonjeza kuti adzakhala ndi Yakobo. ***(Genesis 46: 2-4)***<br>• *Kambiranani momwe Mulungu amakwaniritsira malonjezo ake.*<br>• Yakobo ndi banja lake anachoka ku Beereseba ndi kukhala ku Aigupto. Iwo analipo anthu ambiri! Onse pamodzi analipo anthu 70 amene anakhala ku Aigupto! ***(Genesis 46: 5-27)***<br>• Pamene anafika ku dera la Goseni lomwe linali mbali ya Aigupto, Yosefe anabwera kudzakumana nawo. Iye anasangalala kwambiri kuona abambo ake patapita zaka zambiri. Iye anakumbatira abambo ake ndipo analira nthawi yayitali. Mfumu Farao anamva kuti abwera. Iye anawalandira ndi kuwalola kuti azikhala m'dera la Goseni. ***(Genesis 46: 28-34)***<br>• *Kambiranani mathero abwino a nkhaniyi ndi ana. Fotokozani kuti tikuyenera kudalira Mulungu mu nthawi zabwino ndi mu nthawi zovuta monga anachitira Yosefe. Ife titha kudalira Mulungu kuti abweretsa zabwino mu nyengo zoyipa ngati tingamudalire kwathunthu.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Onse pamodzi mu Aigupto. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Genesis 50: 20***. Gwiritsani ntchito vesi imeneyi pofotokoza nkhani yonse. Kodi abale anachita chiyani pofuna kuzunza Yosefe? Kodi Mulungu anasintha motani zimenezi ndi kukhala zabwino? Onetsetsani kuti ana akumvetsetsa kuti Mulungu ndiye akulamulira zonse m'miyoyo yawo. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.<br>• Kodi banja la Yakobo linkapita kukakhala kuti?<br>• Kodi iwo anayima pati kuti apereke nsembe?<br>• Kodi Mulungu anamulonjeza chiyani Yakobo?<br>• Kodi anabwera kudzakumana nawo atafika ku Goseni ndi ndani?<br>• Kodi ndi anthu angati a banja la Yakobo ankakhala mu Aigupto tsopano?<br>• Zinthu zomvetsa chisoni zinachitika pa moyo wa Yosefe. Kodi Mulungu anachita chiyani kuti kumapeto ake akhale osangalatsa? |

**B8 Nkhani Yoyamba**

**Anthu amene Yesu anakumana nawo: Mayi wodwala – Iyi ndi nkhani ya mphamvu yochiritsa ya Yesu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yesu anachiritsa anthu chifukwa ndiye Mwana wa Mulungu.<br>• Ambuye Yesu atha kuchita zinthu m'miyoyo yathu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Machitidwe 10: 38***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 4: 38-44*** |
| **MAWU OYAMBA** | Uzani ana kuti ayimirire ndi kuchita masewero awa "malo amodzi" – chitsanzo: kulumpha, kuthamanga, kuyenda ndi kuponya manja awo kutsogolo, kapena ngati pali malo okwanira, atha kukhala ngati maloboti a pa msewu. Mukatchula mtundu, ana amvere malangizo: chofiira = ayime, cha olenji = alumphe pa malo amodzi, girini = aziyendayenda. Ana amene alephera kumvera malamulo a pa msewu atuluke mu sewero.<br>Pamapeto fotokozani kuti iwo asangalala pakuti zonse ndi zowayenera. Koma ngati mukudwala sizimasangalatsa chifukwa mukhala mutagona. Mu nthawi ya Yesu, kunali anthu ambiri odwala koma panalibe dokotala kapena mankhawala oti n'kuwachiritsa.<br>Muwazindikire ana amene sangathe kuchita nawo masewerowa pamene mukuyamba. Komanso fotokozani ngati iwo atakhala dokotala lero – kudziwa matenda ambiri, kupereka mankhwala, kukhala otanganidwa, nthawi zinanso kuthandiza anthu komanso nthawi zina osathandiza. Fotokozani kuti mu nkhani ya lero tiphunzira za ntchito yabwino ya dokotala woposa onse – Ambuye Yesu! |
| **PHUNZITSANI** | • Yesu anali mu sunagoge (nyumba imene Ayuda ankasonkhana kuphunzira za Mulungu) kuphunzitsa anthu. Iye anachiritsanso munthu. Tsopano inali nthawi yoti apite ku nyumba ya Simoni pamodzi ndi ophunzira ena. Koma kunali vuto kumeneko. Mpongozi wa Simoni (fotokozani zomwe zikutanthauza) ankadwala kwambiri malungo. *Fotokozani zomwe munthu amamva m'thupi akamadwala malungo – kumva kutentha ndi kuphwanya kwa thupi lonse.* Simoni ndi ena aja ankadziwa kuti Yesu akanatha kumuchiritsa, choncho anafunsa Yesu amuthandize. *N'chifukwa chiyani iwo ankaganiza kuti Yesu angathandize?* ***(Luka 4: 38)***<br>• Yesu anali wofuna kumuchiritsa. Iye anagwira dzanja la mayiyo ndipo anayankhula ndi malungo ndipo anamuthandiza kuyimirira. Nthawi yomweyo anachira ndi kuyamba kupereka chakudya. Zinthu zinakhala ngati kuti palibe chilichonse chimene chinali cholakwika ndi iye! *Funsani ana kuti aganizire zinthu zina zomwe anthu anayankhula kwa wina ndi mnzake.* ***(Luka 4: 39)***<br>• Madzulo pamene dzuwa linkalowa; anthu ambiri anabweretsa odwala ndi amavuto kwa Yesu. *Kambiranani za anthu osiyanasiyana amene anali pamenepo ndi chifukwa chomwe anasonkhanira. Kodi Yesu anamva bwanji pa mapeto a tsiku limenelo? Ngakhale kuti kunali kutada, Yesu anapezabe nthawi yothandiza aliyense.* Iye anasanjika manja aliyense. Palibe amene anachoka osachiritsidwa. *Tsopano kambiranani za zomwe anthu ankachita.* ***(Luka 4: 40-41)***<br>• M'mawa otsatira, Yesu anapeza malo achete pamene anakapemphera kwa Atate ake. Komabe anthu anapitirira kumufunafuna Iye! Iwo ankadziwa za mphamvu yake yodabwitsa. ***(Luka 4: 42)***<br>• *Lero Ambuye Yesu amasamalirabe ndipo akufuna kuti athandize anthu. Iye atha kuchita zabwino m'miyoyo yathu pamene takonzeka kumudalira.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Anthu amene Yesu anakumana nawo: Mayi wodwala. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Machitidwe 10: 38***. Sankhani mawu pa vesi imeneyi molinga ndi msinkhu wa ana a gulu lanu. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.<br>• Kodi Yesu ankachita chiyani m'sunagoge?<br>• Kodi Yesu anapita ku nyumba ya ndani?<br>• Kodi ndani ankadwala malungo?<br>• Kodi Yesu anachita zinthu ziwiri ziti pomuchiritsa?<br>• Kodi iye anachita chiyani atachiritsidwa?<br>• N'chifukwa chiyani anthu ambiri ankabwerabe kwa Yesu?<br>• Kodi m'mawa wa tsiku linalo Yesu anachita chiyani?<br>• Lembani mawu amene palibe, "Yesu anayendayenda ku _______." |

## B8 Nkhani Yachiwiri

**Anthu amene Yesu anakumana nawo: Munthu wakhate – Iyi ndi nkhani ya chikondi cha Yesu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yesu anaonetsa chikondi chake pochiritsa munthu wakhate.<br>• Yesu amatikonda ndipo akufuna kusintha miyoyo yathu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 7: 22***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 5: 12-16*** |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ana kuti atchule matenda opatsirana amene iwo akuwadziwa, monga katsabola ndi chikuku. Yankhulani za kukhala kutali ndi anzanu ndi kusachita nawo zinthu zonse monga kale. Fotokozani kuti mu nthawi ya Yesu, khate anali matenda a pa khungu amene anali opatsirana. Munthu amene ali ndi matenda amenewa sankakhala pakati pa abale ake kapena kugwira ntchito. Panalibe mankhwala ochiza matendawa!<br>Limbikitsa ana kuti aziyamika chifukwa cha chisamaliro cha zaumoyo chomwe lero chilipo – mwina mutha kuyankhula izi kudzera m'pemphero. |
| **PHUNZITSANI** | • Tsiku lina, munthu amene ali ndi khate anabwera pafupi ndi Yesu. Iye anagwa pansi pa mapazi a Yesu ndi kupempha thandizo. Iye anati, "Ambuye, ngati mukufuna, mukhoza kundiyeretsa." Izi zikuonetsa kuti munthu ameneyu ankadziwa kuti Yesu anali ndi mphamvu zomuchiritsa ngati Iye anali wofuna kutero. *Kambiranani zomwe Yesu akanachita. Kodi Yesu ankafuna kuchita chilichonse kwa munthu amene anali ndi nthenda yopatsirana? Kodi Iye akanafuna kuthandiza munthuyu?* ***(Luka 5: 12)***<br>• Kunena zoona, Yesu ankafuna kumuthandiza munthuyo. Iye anamukonda kwambiri ndi kudziwa kuti ankafunika thandizo ndithu. Kenaka Yesu anachita chinthu chabwino kwambiri. Iye anatambalitsa dzanja lake ndi kumukhudza munthu ndi kuti, "Ine ndikufuna. Yeretsedwa!" Yesu sanatenge matenda akhate atakhudza munthuyo koma m'malo mwake munthuyo anachira nthawi yomweyo. *Fotokozani momwe khungu lake linayamba kuonekera komanso ndi kufotokoza kudabwa ndi kuyamika kwa munthuyo.* ***(Luka 5: 13)*** *Ichi chinali chodabwitsa china. Yesu apa anaonetsanso mphamvu yake yayikulu yochiritsa ndi kusintha miyoyo ya anthu.*<br>• Baibulo limafananiza khate ndi tchimo lathu. *Fotokozani kuti tchimo ndi chiyani ndi momwe limaonongera miyoyo yathu. Yesu, amene analibe tchimo, analolera kubwera pa dziko lapansi kudzatipulumutsa tonse ochimwa. Iye amatikonda ngakhale timachita zolakwa. Ngati tili ofuna, Iye adzatikhululukira ndi kutiyeretsa ku tchimo lathu. Miyoyo yathu itha kusintha m'kati mwathu.*<br>• Yesu atachiritsa munthuyu, Iye anamuwuza kuti apite kwa wansembe kuti akadzionetse kuti wachira. *Kodi moyo wake udzakhala wosiyana ndi kale motani?* Munthuyu sakanatha kuyiwala tsiku limene anakumana ndi Yesu. ***(Luka 5: 14)*** Ngati titapempha Ambuye Yesu kuti atikhululukire machimo athu, limeneli lidzakhala tsiku lopambana kwambiri pa miyoyo yathunso.<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Anthu amene Yesu anakumana nawo: Munthu wakhate. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Luka 7: 22***. Vesi ikufotokoza njira zisanu ndi imodzi za momwe Ambuye Yesu amasinthira miyoyo ya anthu. Kuti tilemba mwatsatanetsatane n'kovuta – yesani kugwiritsa ntchito chifaniziro pa mawu aliwonse: monga, kusaona = lozani maso, kusayenda = yendani malo amodzi, amene ali ndi khate = khudzani khungu ndi dzanja lanu. Kapena muyike mawu awa m'magulu awiri ngati akuoneka kutalika. Ana a Kalasi 2 ali ndi chidziwitso chokwanira cha Baibulo atha kupereka zitsanzo za anthu amene Yesu anawachiritsa pa matenda a gulu lililonse. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana ngati ziganizo izi ndi zoona kapena zabodza monga njira yowakumbutsa nkhani.<br>• Khate ndi matenda opatsirana.<br>• Munthuyu ankaloledwa kukhala ndi abale ake.<br>• Iye anagwada pamaso pa Yesu.<br>• Munthu analibe chitsimikizo choti Yesu akanamuchiritsa.<br>• Yesu anamukhudza.<br>• Yesu anatha kuchiritsa munthuyu chifukwa anali Mwana wa Mulungu.<br>• Iye anachiritsidwa patapita kanthawi pang'ono.<br>• Iye anayenera kupita kukadzionetsa kwa wansembe.<br>• Tonse tili ndi nthenda yotchedwa tchimo.<br>• Ambuye Yesu amatikonda tonse ndipo ndi wokonzeka kutikhululukira tchimo lathu. |

## B8 Nkhani Yachitatu

**Anthu amene Yesu anakumana nawo: Munthu wosowa thandizo – Iyi ndi nkhani ya ku khululukira kwa Yesu.**

**Ife tikuphunzira kuti:**
- Yesu anali ndi mphamvu osati zongochiza munthu wolumala komanso kukhululukira machimo ake.
- Yesu ali ndi mphamvu yokhululukira machimo.

**Vesi Yoloweza:** ***Luka 5: 24***
**Ndime Yowerenga:** ***Luka 5: 17-26***

**MAWU OYAMBA**

Funsani ana kuti akufotokozereni zomwe angachite pofuna kuthandiza mnzanu ku sukulu kapena ku nyumba. Yamikirani thandizo lawo. Mu nkhani yathu ya lero, anthu anayi ananyamula mnzawo amene sankatha kuyenda kwa Yesu. Ngati n'kotheka, mutenge mphasa kuti chikhale chitsanzo pamene mukufotokoza zomwe anthuwa anachita. N'chifukwa chiyani anabwera naye kwa Yesu? Inde, iwo ankadziwa kuti Yesu anali ndi mphamvu zochiritsa mnzawoyo.

**PHUNZITSANI**

- Koma kufika pamene panali Yesu kunali kovuta kwambiri. Kunabwera anthu ochuluka kwambiri kudzamva Yesu akuyankhula. *N'kofunika kwambiri kwa ife kumva mawu a Yesu.* Kunali kosatheka kuti alowe naye pa khomo choncho anamunyamula ndi kukwera naye pa denga la nyumbayo. Iwo sanali okonzeka kuchoka osaonana ndi Yesu chifukwa ankadziwa kuti ndi yekhayo amene akanawathandiza! *Funsani ana aganizire zomwe zimachitika anthu akayimirira m'nyumba kenaka ndi kuona bowo pa denga la nyumbayo kenaka ndi kuona munthu akulowetsedwa mpaka pa mapazi a Yesu.* ***(Luka 5: 18-19)***
- *Kodi Yesu amuchiritsa motani munthuyu? Funsani ana kuti akumbukire nkhani ya kuchiritsidwa kwa mpongozi wa Petro ndi munthu wakhate.* Koma pa nkhani ya lero, Yesu akuyankhula kwa munthuyo kuti, "Mnzanga, machimo ako akhululukidwa." Anthu ena amene anali m'nyumbamo anakwiya. Iwo sankakhulupirira kuti Yesu angakhululukire machimo. Iwo ankaganiza kuti ndi Mulungu yekha amene angakhululukire machimo ndipo sankakhulupirira kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu. Yesu ankadziwa zomwe ankaganiza. Iye amadziwanso maganizo athu! ***(Luka 5: 20-24)***
- Yesu anafuna kuwaonetsa kuti anamukhululukira munthuyu machimo ake ngakhale kuti iwo sankatha kuona pa moyo wake! Motero, Iye anawuza munthu wosowa thandizoyu kuti anyamule mphasa yake ndi kupita kwawo. Nthawi yomweyo munthuyo anachita zimenezi ndi kupita kwawo akuyamika Mulungu! Aliyense anadabwa. Mphamvu ya Yesu sinangochiritsa kokha komanso anakhululukira machimo ake! Palibe wina aliyense anali ndi mphamvu ngati imeneyi! ***(Luka 5: 24-26)***
- Chosowa chathu chachikulu ndi kukhululukidwa machimo athu. *Kumbutsani ana zomwe anaphunzira mu Nkhani Yachiwiri – tchimo ndi chiyani, limaononga motani ubale wathu ndi Mulungu ndi kutilephretsa ife kupita Kumwamba.* Ambuye Yesu ali ndi mphamvu zokhululukira machimo athu chifukwa Iye analibe tchimo. Iye anali wokonzeka kufa pa mtanda kuti alangidwe chifukwa cha tchimo lathu. Ife tikuyenera kulapa kwenikweni ndi kuyamika Ambuye Yesu potipatsa njira yoti tikhululukidwe.

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Anthu amene Yesu anakumana nawo: Munthu wosowa thandizo.

**PHUNZIRANI**

Phunzitsani Vesi Yoloweza yomwe ndi mbali imodzi ya nkhaniyi: ***Luka 5: 24***. Fotokozani kuti "Mwana wa Munthu" ndi dzina lina lina la Ambuye Yesu.

**KUMBUKIRANI**

Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.
- Kodi munthuyu anali ndi abwenzi angati?
- Kodi vuto la munthuyu linali chiyani?
- N'chifukwa chiyani anzake ankalephera kufika naye kumene kunali Yesu?
- Kodi anachita chiyani kuti alowe naye m'nyumbamo?
- Kodi Yesu anati chiyani kwa munthuyo nthawi yoyamba?
- N'chifukwa chiyani anthu ena anakwiya?
- Kodi Yesu anachita chiyani pofuna kuonetsa kuti wakhululukira munthuyo?
- Kodi ndi chinthu chofunika chiti chomwe Ambuye Yesu angatichitire?

## B8 Nkhani Yachinayi

**Anthu amene Yesu anakumana nawo: Mateyu – Iyi ndi nkhani ya kutsatira Yesu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yesu ankadziwa kuti moyo wa Mateyu unali wotani, koma Iye anafuna kuti amutsatire.<br>• Yesu akufuna kuti ife timutsatire.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 5: 32***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 5: 27-32*** |
| **MAWU OYAMBA** | Mukambirane ndi ana za mitundu ya ntchito imene akufuna adzagwire akadzakula. Unikani kuti muone ubwino wa ntchito zimenezi.<br>**Kapena**<br>Chitani zionetsero zina za ntchito zimene anthu amagwira m'dera lanu kuti ana atchule kuti ntchito imeneyo ndi yotani.<br>Fotokozani kuti nkhani ya lero ndi ya munthu wotchedwa Mateyu (Levi) amene anali wolandira misonkho. Iye anakhala m'mbali mwa msewu ndi kumalandira ndalama zomwe iye ankapereka kwa Aroma amene ankalamulira dziko. Mutha kuwafotokozera ana kuti ngakhale lero timapereka misonkho ndi ntchito zake.<br>Mwachisoni, palibe amene ankakonda Mateyu. Anthu ankadana ndi aliyense wolandira misonkho chifukwa ankagwirira ntchito adani awo (Aroma) komanso chifukwa nthawi zina ankalandira ndalama zoposa muyeso, zomwe iwo ankasunga. |
| **PHUNZITSANI** | • *Tsiku lina Yesu anaona Mateyu akugwira ntchito yake. Ganizirani zomwe Yesu ankaganiza za Mateyu - Kodi Iye ankadziwa kuti Mateyu anali munthu wotani? Inde ankadziwa ...Iye amadziwa chilichonse cha aliyense wa ife. Kodi Yesu anali ndi cholinga ndi moyo wa Mateyu? Inde! Mateyu anali mtundu wa anthu amene Yesu anabwera kudzawathandiza - Iye akanatha kusintha moyo wa Mateyu!* Choncho, Iye anayima pamene pali Mateyu ndipo anati, "Tsate Ine." ***(Luka 5: 27)*** *Kodi Mateyu akanachita chiyani? Fotokozani chisankho chimene Mateyu ankayenera kuchita.*<br>• Mateyu anadziwa nthawi yomweyo chomwe ankayenera kuchita. Iye ankayenera kutsatira Yesu! Zinali zabwino kuti Yesu anamuyitana! Iye anayimirira ndi kusiya chilichonse ndi kupita ndi Yesu. ***(Luka 5: 28)*** *Fotokozani kuti Ambuye Yesu akuyitana aliyense wa ife kuti timutsatire ndi kuti Iye akhale m'moyo wathu. Ifenso tikuyenera kuchita chisankho.*<br>• Mateyu anafuna kuti anzake akumane ndi Yesu komanso kuti adziwe momwe moyo wake wasinthira. Choncho, iye anawayitana pamodzi ndi Yesu ndi ophunzira ake ku chakudya ku nyumba kwake. Anthu ena amene anali pamenepo ankaganiza kuti Yesu ankalakwitsa kukhala pamodzi ndi Mateyu ndi anzakewo. Iwo ankaganiza kuti Yesu ankayenera kumakhala pakati pa anthu abwino osati ochimwa. Iwo sankazindikira kuti aliyense ndi wochimwa. Yesu anawafotokozera cholinga chake chobwera pa dziko lapansi – sanabwerere anthu amene ankaganiza kuti ndi abwino koma chifukwa cha amene ankadziwa kuti anali ochimwa ndipo ankafuna kulapa machimo awo. ***(Luka 5: 29-32)*** Yesu sakonda tchimo koma amakonda ochimwa monga Mateyu ndi ife! Ife tikuyenera kumukhulupirira kuti atikhululukire kenako kumutsatira.<br>• Pambuyo pake, Mulungu anasankha Mateyu kuti agwire ntchito yofunika kwambiri. Iye analemba buku loyamba la Chipangano Chatsopano. Linali tsiku lopambana kwambiri pamene anachita chisankho chotsatira Yesu ndi kulola Yesu kuti achotse makhalidwe oyipa m'moyo wake. Kuyambira nthawi imeneyi, moyo wake unasintha.<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Anthu amene Yesu anakumana nawo: Mateyu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Luka 5: 32***. Fotokozerani mawu ovuta, monga 'kulungama' ndi 'kutembenuka mtima'. |
| **KUMBUKIRANI** | Muli m'kalasi, ana akhale ndi zithunzi za anthu osiyanasiyana amene Yesu anakumana nawo mu nkhani zathu. Kapena mutha kukhala ndi mafunso pofuna kubwereza zonse za mu B8, omwe musankhe kuchokera pa zomwe mwaphunzira kale ndi za Mateyu: monga,<br>• Kodi Mateyu ankagwira ntchito yotani?<br>• Kodi Yesu anati chiyani kwa Mateyu?<br>• Kodi Mateyu anachita chiyani atayamba kutsatira Yesu? |

## B9 Nkhani Yoyamba

**Kubadwa kwa Mose – Iyi ndi nkhani ya momwe Mulungu amasamalira anthu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Mulungu anasamalira Mose, ndipo amasamalira ifenso. (Kalasi 1)<br>• Mulungu anali ndi cholinga ndi moyo wa Mose monga ali ndi cholinga ndi ifenso. (Kalasi 2)<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Ahebri 11: 23***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 2: 1-10*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yambani ndi kufotokoza ndondomeko imene ana atha kuyidziwa - monga: ndondomeko ya sukulu kumene kumakhala zochitika zambiri motsata. Fotokozani kuti Mulungu ali ndi cholinga ndi miyoyo yathu. M'banja m'mene tinabadwira zinthu zomwe zimatichitikira sizimakhala mopanda cholinga – Mulungu amagwiritsa ntchito zimenezi pofuna kutikonza kuti tidzamutumikire. M'nkhani izi tiphunzira za Mose. Mulungu anali ndi ntchito yofunika kwambiri yoti Mose adzagwire akadzakula. Lero tiphunzira momwe Mulungu anasamalira Mose ali mwana. Nkhani imeneyi ikupezeka m'buku lachiwiri la m'Baibulo. Funsani ngati alipo amene akudziwa bukuli ndipo aonetseni pamene lili.<br>Komanso ngati mukuyamba kuwafotokozera nkhaniyi kwa ana a Kalasi 1, mutha kuyankhula za makanda mwinanso kukhala ndi zomwe makanda angaseweretse ndi kutetezedwa. |
| **PHUNZITSANI** | • Fotokozani mwachidule mbiri ya Aisrayeli (Ahebri) monga akapolo – onani mawu oyamba a phunziro la Kalasi 2. ***(Eksodo 1: 1-11)*** Mfumu Farao anayesetsa kuti achepetse chiwerengero cha Aisrayeli kuti chisachuluke, motero iye anaganiza zoti aziponya mu Mtsinje wa Nailo ana onse aamuna Aisrayeli. ***(Eksodo 1: 22)*** *Kodi bambo ndi mayi wa Chisrayeli ankamva bwanji mu mtima akabereka mwana wamwamuna?*<br>• M'nyumba ina, munabadwa mwana wamwamuna wokongola ndi wathanzi. Makolo ake anamubisa m'nyumba kukhulupirira kuti Mulungu adzamuteteza. Koma patapita miyezi itatu, iwo sakanathanso kumubisa. *N'chifukwa chiyani sakanatha?* Mayi ake anapanga dengu la mabango ndi kumata phula kuti madzi asalowe *(fotokozani)*, anayikamo mwanayo ndi kukabisa dengulo m'mbali mwa mtsinje pa mabango. Miriamu, mlongo wa mwanayo anatsala kumeneko kuti aziona zomwe zichitike ndi mwanayo, koma Mulungu ndiye amene ankamuteteza mwanayo. ***(Eksodo 2: 1-4)***<br>• Fotokozani gawo lotsatira la nkhani kudzera mu sewero – fotokozani momwe Miriamu anaonera mwana wamkazi wa Farao ndi amene ankamuthandiza akubwera. Kodi amuona mwanayo? Kodi akawuza mfumu? Inde, mwana wamkazi wa Farao anaona dengulo ndipo anawuza womuthandiza ake kuti akatenge. Fotokozani zomwe iye anachita ataona mwana wa Chihebri m'dengumo. Mwana wamkazi wa Farao sanafune kuti mwanayo aphedwe! Mulungu ndiye ankateteza mwanayo! ***(Eksodo 2: 5-6)***<br>• Kenaka Miriamu anatuluka ndi kudzipereka kuti akapeze mayi oti asamalire mwanayo. *Kodi iye akapeza ndani?* Mwana wamkazi wa Farao anavomera ndipo Miriamu anathamanga kupita kukapeza mayi ake a mwanayo! Choncho mayi a mwanayo anayang'anira mwanayo m'nyumba mwake mwaufulu chifukwa mwana wamkazi wa mfumu anali atavomereza. Pambuyo pake, pamene mwanayo anakula, mwana wamkazi wa mfumu anamutenga ndi kukhala naye m'nyumba yaufumu ya Farao. Iye anamutenga ndi kukhala mwana wake ndipo anamutcha Mose, kutanthauza "ndinamuvuula m'madzi". ***(Eksodo 2: 7-10)*** Tsopano Mose anakhala mwana wa mfumu ya Aigupto!<br>• *Thandizani ana kuti amvetsetse kuti Mulungu ankalamulira zochitika zonsezi. Molingana ndi lamulo la Farao, mwanayo ankayenera kuponyedwa m'madzi. Makolo a Mose ankakhulupirira Mulungu – iwo anadalira Mulungu kuti asamalira mwana wawoyo ndipo Iye anatero. Ichi chinali chiyambi chabe cha chikonzero cha Mulungu. Mulungu akufuna kuti ife timudalire kuti akwaniritsa zolinga zake pa miyoyo yathu.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kubadwa kwa Mose. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Ahebri 11: 23*** (Kalasi 2). Ana a Kalasi 1 aphunzire gawo loyamba la vesi. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.<br>• Kodi nkhani ya Mose ikupezeka m'buku liti?<br>• Kodi Farao analamula kuti ana onse aamuna a Chihebri achite nawo chiyani?<br>• Kodi anamubisa mwanayo m'nyumba miyezi ingati?<br>• Kodi amayi ake anapanga chiyani?<br>• Kodi anamuyika mwanayo muti?<br>• Kodi ndani anakhala m'mbali mwa mtsinje kuyang'anira mwanayo?<br>• Kodi ndani anapeza mwanayo?<br>• N'chifukwa chiyani moyo wa Mose sunalinso pa chiopsezo kuyambira nthawi imeneyi?<br>• Kodi ndani anaonetsa chikhulupiriro mu nkhani imeneyi?<br>• Kodi ndani ankateteza Mose? |

## B9 Nkhani Yachiwiri

**Cholakwa chachikulu cha Mose – Iyi ndi nkhani yakuti Mulungu amaona chilichonse.**

**Ife tikuphunzira kuti:**
- Mose analakwitsa pamene anachita zinthu mwachangu komanso mwa mkwiyo.
- Ife sititha kuthawa zotsatira za zinthu zoyipa zomwe timachita.

**Vesi Yoloweza:** ***Numeri 32: 23***
**Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 2: 11-15***

**MAWU OYAMBA**

Nthawi zina timaganiza kuti timadziwa zonse. Sankhani chitsanzo chomwe mwana angathe kuchita mothandizidwa ndi munthu wamkulu, koma mwanayo achite monga m'mene akudziwira koma sakwanitsa! Sabata yatha tinaphunzira za Mose. *Funsani mafunso pofuna kuwakumbutsa.* Kodi Mose anapita kukhala kuti pamene anali mnyamata? Kodi anthu a mtundu wake anali ati? (Aisrayeli/Ahebri) Kumbutsani ana kuti iwo anali akapolo ndipo ankachitidwa nkhanza ndi Aaigupto. Mu nkhani yathu ya lero Mose wakula. Mvetsetsani kuti muphunzire za nthawi imene Mose ankayesa kuti inali yabwino kwambiri.

**PHUNZITSANI**

- Tsiku lina Mose anapita kukaona abale ake. Nthawi imeneyo anaona m'bale wake mmodzi akumenyedwa ndi Maigupto. *Kodi Mose anamva motani mu mtima mwake?* (anakwiya, anafuna kuteteza anthu ake) Nthawi yomweyo Mose anayang'ana uku ndi uku kuti aone ngati wina akumuona, ndipo anapha Maiguptoyo. Kenaka anakwirira thupi lake mu mchenga. Mose anaganiza kuti wachita chinthu choyenera, koma kodi anachitadi? *Athandizeni ana kuti azindikire kuti Mose anachita zolakwika. (Kalasi 2: Mutha kufotokozanso momwe Mulungu amaonera zolakwa zomwe Aaigupto ankachita ndi kufotokoza momwe Mulungu adzachitire ndi anthu olakwa m'tsogolo.) Kodi mukuganiza kuti Mose sangalandire chilango chifukwa cha zomwe wachita? Ngati si choncho, n'chifukwa chiyani?* ***(Eksodo 2: 11-12)***
- Tsiku lotsatira Mose anaona Ahebri awiri akumenyana. Pamene anafunsa zomwe zinkachitika, mmodzi mwa anthuwo anati, "Kodi ndani anakuyika kuti ukhale wotilamulira ndi wotiweruza? Kodi ukufuna kundipha monga momwe unaphera Maigupto uja?" Tsopano Mose anazindikira kuti anamuona pamene ankapha Maigupto uja. *Kodi iye anamva chiyani mu mtima mwake? (anachita mantha kuti mfumu imva nkhaniyi)* Mosachedwa Farao anamva zomwe anachita Mose ndipo anafuna kumupha. Mose anathawa kupita ku dziko lina la Midyani kumene ankagwira ntchito ngati m'busa wa ziweto za Yetero. ***(Eksodo 2: 13-22)***
- Mulungu ankadziwanso zolakwa zomwe Mose anachita. *Fotokozani kuti Mulungu amaona chilichonse timachita ndipo sitingathe kubisa zolakwa zathu pamaso pake. Ngakhale Mose anali atakula tsopano, iye anachita zolakwa ndipo sanachite zolondola. Iye anali ndi zambiri zoti aphunzire asanakhale mtsogoleri. Ife tikuyenera kuphunzira kuchokera pa zolakwa za Mose ndi kudalira Mulungu kuti azitithandiza kuchita zoyenera zomwe zimamukondweretsa.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Cholakwa chachikulu cha Mose.

**PHUNZIRANI**

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Numeri 32: 23***. Lumikizani vesiyi ndi kulakwa kwa Mose. Kodi tchimo la Mose linali lotani? Nanga anthu anadziwa bwanji? Mutha kupereka nkhani yochitika ya munthu amene anapezeka atalakwa chomwe ana angathe kumvetsa.

**KUMBUKIRANI**

Gwiritsani ntchito mawu akuti zoona/zabodza pa ziganizo izi:
- Mose anapha Mhebri.
- Iye ankaganiza kuti palibe amene ankamuona.
- Mhebri wina anamuona.
- Mulungu anaona zomwe zinachitika.
- Farao anayika Mose m'ndende.
- Mose anali ndi zinthu zambiri zoti aphunzire asanakonzeke kukhala mtsogoleri.

**B9 Nkhani Yachitatu**

**Mose aona chitsamba chikuyaka moto – Iyi ndi nkhani ya kumvera zomwe Mulungu akunena.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Mose anali mtsogoleri amene sankafuna koma Mulungu anamulonjeza kumuthandiza.<br>• Mulungu ndi woyera ndipo tikuyenera kumakumbukira chimenechi.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 3: 12***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 3:1 - 4: 17*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za kufunsidwa mutachita kanthu kofunika kwambiri ndi kokondweretsa, monga, udindo woyenerana ndi anawo m'magulu anu. Kodi munamva bwanji mu mtima pamene munafunsidwa kuti muchite izi? *(mantha / kufuna kuti wina ndiye achite?)*<br>Lero patapita zaka makumi anayi kuchokera nthawi imene Mose anachita cholakwa chachikulu. Mose anali m'busa wa ziweto m'chipululu zaka makumi anayi. Mulungu sanamuyiwale. Iye anali wokonzeka kumukhululukira ndi kumupatsa ntchito yatsopano kuti agwire. |
| **PHUNZITSANI** | • Tsiku lililonse linali lofanana kwa iye, koma tsiku lina... Mose anaona chitsamba chikuyaka moto. Chodabwitsa n'chakuti ngakhale chinkayaka moto, masamba ndi nthawi sizinkanyeka! Mose anayandikira kuti aone ndipo kenaka Mulungu anayitana dzina la Mose. *Gwiritsani ntchito mawu ochokera m'Baibulo kuti mufotokoze gawo lotsatira. Fotokozani kuti "malo opatulika" ndi malo apadera kwambiri chifukwa panali Mulungu. Tikuyenera kumvetsa kuti Mulungu ndi woyera ndi wosiyana ndi ife. Mosiyana ndi ife, Mulungu alibe tchimo.* Mose anavula nsapato zake ndi kubisa nkhope yake chifukwa ankamvetsa za ukulu wa Mulungu. ***(Eksodo 3: 1-6)***<br>• *Thandizani ana kuti akumbukire m'mene moyo wa Aisrayeli unalili mu Aigupto.* Mulungu anawuza Mose kuti ankadziwa zoyipa zonse zimene zinkachitika ndipo tsopano inali nthawi yoti awatulutse mu Aigupto ndi kupita ku dziko latsopano. Mulungu anafuna Mose kuti akhale mtsogoleri wawo ndi kuti apite akayankhule ndi Mfumu. *Kambiranani zomwe Mose ankamva mu mtima mwake pa nkhani yobwerera ku Aigupto.* ***(Eksodo 3: 7-10)***<br>• *Lumikizani zomwe ana ayankha pa mawu oyamba aja ndi kuona ngati analondola pamene amanena za momwe Mose anamvera mu mtima mwake pa za kukhala mtsogoleri. Kenaka lumikizani kukana kwa Mose ndi zomwe Mulungu anayankhula zomwe zili m'Baibulo pa ndime imene tawerenga komanso m'mabokosi amene ali mu phunziro la Kalasi 2. Kwa Kalasi 2, mutha kulemba zimenezi m'magawo awiri pa bolodi kapena pa chipepala.*<br>• Ine ndine munthu wosayenera – Ine ndidzakhala nawe. ***(3: 11, 12)*** Ine sindikudziwa dzina lanu – Dzina langa NDINE (dzina ili limasonyeza kuti Mulungu ndi wamphamvuzonse). Ine ndine Mulungu wa makolo ako, Mulungu wa Abrahamu. ***(3: 13-15)*** Iwo sadzandikhulupirira – Ine ndidzakupatsa mphamvu zochitira zodabwitsa. ***(4: 1-9)*** Ine sindidzatha kuyankhula bwino – Ine ndidzakuthandiza kuyankhula ndi kukuphunzitsa zoti uyankhule. ***(4: 10-12)*** Chonde tumizani munthu wina – Aroni adzakuthandiza ndipo iwe udzamuwuza zoti ayankhule. ***(4: 13)***<br>*Kodi inu mukuganiza kuti Mose anali munthu woyenera kukhala mtsogoleri? Kodi mukuganiza kuti Mulungu ankakondwera ndi zifukwa zimene ankapereka? Ayi!* Koma ngakhale m'mbuyomo ku Aigupto analakwitsa pamodzi ndi zifukwa zake, iye anali munthu amene Mulungu anamusankha. Mu nkhani yathu yotsatira tidzaphunzira momwe Mose pomaliza anakhala wokonzeka kumvera ndi kuti Mulungu anatha kukwaniritsa chifuniro chake pa moyo wake. Mose ankayenera kudalira Mulungu pa chilichonse chinali m'tsogolo mwake.<br>• *Nthawi zina Mulungu amatiwuza tigwire ntchito yake yomwe imaoneka ngati yovuta. Ife tikuyenera kukumbukira kuti Iye ali ndi ife ndipo adzatithandiza.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Mose aona chitsamba chikuyaka moto. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Eksodo 3: 12a***. Iyi ndi vesi yayifupi itatha nkhani yayitali. Ana atha kukonda atayilemba pa pepala ndi kuyika m'Baibulo kapena kuyilemba pa pepala lalikulu ndipo mwana aliyense achekenire chilembo chilichonse. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.<br>• Kodi chinthu chimene Mose anaona chachilendo pa chitsamba ndi chiyani?<br>• Kodi Mose anachita chiyani pamene anali pa malo opatulika?<br>• Kodi mawu akuti kupatulika akutanthauza chiyani?<br>• Kodi Mulungu ankafuna kuti Mose akagwire ntchito yanji?<br>• Perekani zifukwa zokanira zomwe Mose anapereka.<br>• Kodi Mose anapereka chifukwa chotani chokhudzana ndi Mulungu?<br>• Kodi Mulungu analola kuti Mose apite ndi ndani?<br>• Mulungu sanakhumudwe naye Mose. N'chifukwa chiyani sanatero? |

**B9 Nkhani Yachinayi**

**Mose abweretsa uthenga wa Mulungu – Iyi ndi nkhani ya kukhala wokonzeka kugwira ntchito ya Mulungu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Pamapeto pake Mose anamvera zomwe Mulungu anamuwuza kuti achite.<br>• Mulungu anasunga malonjezo ake ndipo adzachita zomwezo kwa ifenso.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 4: 15b***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 3:11-22; 4: 1-31*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za kusintha kofunika m'miyoyo yathu: monga, kulowa nyumba yatsopano, kupita ku sukulu yatsopano, kukwatira. Zinthu zambiri zinasintha pa moyo wa Mose – kumbukira miyezi yoyamba ali khanda, kenaka kukakhala m'nyumba yaufumu ya Farao mpaka pamene anafika zaka makumi anayi, kenaka anakhala m'chipululu zaka zina makumi anayi. (M'kalasi mutha kuyika zithunzi za zomwe zinachitika nthawi zosiyana pa moyo wa Mose.) Tsopano Mose ali ndi ntchito yofunika kwambiri pa moyo wake. Kodi Mulungu anamuwuza kuti achite chiyani? |
| **PHUNZITSANI** | • Mose tsopano anali ndi mkazi ndi ana awiri aamuna m'dziko la Midyani. Iye anapempha apongozi ake Yetero ngati angamulole abwerere ku Aigupto. Yetero anavomera, ndipo Mose ananyamuka pamodzi ndi mkazi wake ndi ana ake amene anakwera pa bulu. Mose anatenganso ndodo yake ija imene Mulungu anamuwuza kuti aziyigwiritsa ntchito. Mulungu anawuza Mose kuti anthu amene ankafuna kumupha pamene anali ku Aigupto anamwalira. Mulungu ankathandiza Mose kuti asachite mantha. Apa Mulungu ankakwaniritsa lonjezo lake pa Mose. *Kodi mukumbukira vesi yoloweza ya sabata yatha?* ***(Eksodo 4: 18-20)***<br>• Kenaka Mulungu anakwaniritsanso lonjezo lina limene anachita kwa Mose. Mose ali paulendo umenewu, m'bale wake Aroni anabwera kudzakumana naye. *N'chifukwa chiyani Aroni anakakumana ndi Mose?* Mose anafotokozera Aroni zonse zimene Mulungu anamuwuza kuphatikiza zizindikiro zimene anamupatsa kuti achite ndodo yake. *Tikuyenera nthawi zonse kukhulupirira kuti Mulungu adzakwaniritsa malonjezo ake onse. Ngati ndinu wake, Iye adzachita zimenezi kwa ife.* ***(Eksodo 4: 27-28)***<br>• Pamene anafika mu Aigupto, Mose ndi Aroni anakumana ndi atsogoleri a Aisrayeli ndipo anawafotokozera zolinga za Mulungu. Kenaka anthu onse anasonkhana ndipo Mose anawaonetsa zodabwitsa zomwe Mulungu anamuwuza kuti achite ndi ndodo yake. Mose anaponya ndodo yake pansi ndipo inasanduka njoka, kenaka, atagwira tchira wake, inasandukanso ndodo. Kenaka analowetsa dzanja lake m'malaya ake ndipo atalitulutsa linali la khate *(fotokozani)* koma atalilowetsanso linachiritsidwa. ***(Eksodo 4: 6-9)*** Pamene anthu anaona zodabwitsazi, anatha kuona mphamvu ya Mulungu ndi kumvetsetsa kuti Mose anatumidwa ndi Mulungu. *Kodi mukuganiza kuti anthu anamva bwanji mu mtima mwawo? (kudabwa / kusangalala kwambiri kuti Mulungu awapulumutsa mu ukapolo)* ***(Eksodo 4: 29-31)***<br>• Mose anali wosangalala kwambiri poona Mulungu akumukonzera njira pamene ankabwerera ku Aigupto. Onaninso za anthu amene anathandiza pa chikonzero cha Mulungu – Yetero, Aroni, atsogoleri, ndi anthu. *Kodi ndi ndani amene anatsala kuti Mose andi Aroni afotokozere cholinga chawo? Tsindikani kuti ngakhale zidzakhala zovuta, iwo adzayenera kudalirabe Mulungu kuti akwaniritse zonse. Iye ndiye amalamulira!*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Mose abweretsa uthenga wa Mulungu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Eksodo 4: 15b***. Onetsetsani kuti ana akumvetsetsa zomwe zikuchitika pamene pali vesi imeneyi yomwe ikufotokoza za Mose ndi Aroni kugwira ntchito pamodzi ndiponso Mulungu kukhala nawo. |
| **KUMBUKIRANI** | Bwerezani kuona moyo wa Mose mpaka pamene wafika pogwiritsa ntchito mafunso ochokera mu nkhani za pambuyo ndiponso awa a mu Nkhani Yachinayi:<br>• Kodi ndi ndani anabwerera pamodzi ndi Mose ku Aigupto?<br>• Kodi ndi ndani anakumana nawo m'njira?<br>• Kodi anthu anadziwa bwanji kuti ndi Mulungu amene anatuma Mose?<br>• Fotokozani chodabwitsa chimodzi chimene Mose anachita pamaso pa anthu. |

## B10 Nkhani Yoyamba

**Mose ndi mliri woyamba – Iyi ndi nkhani ya kumvera Mulungu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Tikuyenera kumvetsera ndi kumvera zomwe Mulungu walamula.<br>• Kukana kumvetsera ndi kusamvera Mulungu kumabweretsa chilango nthawi zonse.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Yeremiya 38: 20 kapena Eksodo 7:16***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 7: 1-24*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani ndi ana malamulo amene tikuyenera kumvera ndi zotsatira zake ngati sitimvera, pa sukulu kapena pakati pa anthu ena. Ndi zothandiza kubwereza Nkhani 4 ya B9 ndi kuona mafunso ochepa amene akugwirizana ndi phunziro la lero. |
| **PHUNZITSANI** | • Tsopano nthawi yakwana yoti Mose ndi Aroni apemphe Farao kuti alole Aisrayeli apite akapembedze Mulungu m'chipululu. *Funsani ana aganiza za yankho la Farao. Fotokozani za kukana kwake ndi zotsatira zake zomwe zinachititsa miyoyo yawo kukhala yovuta kuposa poyamba. Thandizani ana kuti azindikire kuti Farao sakumvera Mulungu. Kodi inu mukanaganiza chiyani za Mose ngati mukanakhala Mwaisrayeli?* ***(Eksodo 5: 1-21)***<br>• Mose sankamvetsa chifukwa chomwe Mulungu analolera kuti zinthu zichitike motere. Iye anafunsa Mulungu za ichi. Mulungu anawalonjeza kuti adzaonetsa mphamvu zake ndipo ngakhale poyamba Farao sakumvera, pamapeto pake Mulungu adzachita kuti iye achite zomwe Mulungu akumuuwuza. *Kumbutsani ana kuti ife timalonjeza ndi kuyiwala kapena sitisunga malonjezo athu. Koma Mulungu adzasunga malonjezo ake nthawi zonse.*<br>• Mulungu anawawuza kuti apitenso kwa Farao ndi kumuwuza kuti alole akapolo Aisrayeli kuti apite! ***(Eksodo 5: 22-7:5)***<br>• Nthawi iyi, Farao anapempha chodabwitsa ndipo ndodo ya Aroni inasanduka njoka. Amatsenga a Farao anachitanso zimenezi, koma ndodo ya Aroni inameza njoka za amatsengawo. *Kodi izi zinaonetsa chiyani za Mulungu?* Komabe Farao sanamvere Mulungu. ***(Eksodo 7:8-12)***<br>• Kenaka Mulungu anawuza Mose ndi Aroni kuti akakumane ndi Farao ku Mtsinje wa Nailo. Iwo anaperekanso lamulo la Mulungu. Ngati Farao samvera, madzi a Mtsinje wa Nailo adzasanduka magazi ndipo sipadzakhala madzi abwino akumwa komanso nsomba zonse zidzafa. Farao anakana kumvera. Baibulo likuti iye anatembenuka ndipo anapita ku nyumba yake. *Kambiranani khalidwe la Farao – ndi mawu ati amene akufotokoza za khalidwe lake? Fotokozani kuti Baibulo likunena kuti anali ndi mtima wouma.* ***(Eksodo 7: 14-23)***<br>• Choncho, Aaigupto anakumba zitsime m'mbali mwa mtsinje kuti apeze madzi akumwa chifukwa sakanatha kumwa madzi a mu mtsinje. Uwu unali mliri woyamba ndipo unakhala masiku asanu ndi awiri. ***(Eksodo 7: 24-25)***<br>• *Mose ndi Aroni anachita zomwe Mulungu anawawuza kuti achite, kumvera zonse mwatsatanetsatane. Izi ndi zimene tikuyenera kuyesetsa kuchita nthawi zonse. Baibulo limati Mulungu amakondwera ife tikamumvera! Farao sanamvere Mulungu ndipo anakana kumumvera, ndipo nthawi zonse zimatha movuta komanso ndi chilango cha Mulungu. Kambiranani zomwe Mulungu amatilamula kuti tichite pa moyo wathu tsiku ndi tsiku.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera – Mose ndi mliri woyamba. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Yeremiya 38: 20 kapena Eksodo 7:16***. Tsindikani kuti Mose ndi Aroni anamvera koma Farao sanamvere. Koma tonse tikuyenera kumamvera Mawu a Mulungu tsiku ndi tsiku. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.<br>• Kodi ndi lonjezo lotani limene Mulungu anachita kwa Mose ndi Aroni?<br>• Kodi chodabwitsa choyamba chomwe Aroni anachita chinali chotani?<br>• Kodi chinachitika ndi chiyani mu Mtsinje wa Nailo pa mliri woyamba?<br>• Kodi ndi chiyani chomwe Aaigupto analibe kwa masiku asanu ndi awiri?<br>• Kodi ndi zinthu ziti zomwe Mulungu amatilamula kuti tizichita tsiku ndi tsiku m'miyoyo yathu? |

## B10 Nkhani Yachiwiri

**Mose ndi mliri wotsiriza – Iyi ndi nkhani ya chikonzero cha Mulungu chopulumutsa Ahebri.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Farao ndi Aaigupto akuyenera kulangidwa chifukwa chokana kumvera Mulungu.<br>• Mulungu salekerera tchimo koma amapereka njira yopulumukira.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 12: 13***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 11: 1-10; 12: 1-13*** |
| **MAWU OYAMBA** | Kambiranani za chitetezo chathu mu nyengo zina. Sankhani chitsanzo chimene ana akuchidziwiza. Mwa chitsanzo: chipewa chimene chimateteza mutu ku dzuwa, pasipoti imatithandiza kulowa m'dziko lina mopanda mantha kapena kumangidwa, katemera amatiteteza kuti tisatenge matenda. M'nkhani ya lero, tiphunzira chizindikiro chimene Mulungu anapereka kwa Aisrayeli kuti akhale otetezedwa ku chilango chake. |
| **PHUNZITSANI** | • Kwachitika kale miliri isanu ndi inayi ndipo nthawi zonsezi Farao wakhala akukana kulola Aisrayeli kuti apite. Mulungu ankaumitsa mtima wa Farao mpaka pamene Farao anazindikira ukulu wa Mulungu.<br>• Farao anali atawuza Mose kuti sakufuna kuonanso nkhope yake. ***(Eksodo 10: 27-29)*** Koma Mulungu anali atawuza Mose mliri wotsiriza kuti udzakhala wotani. Kudzakhala chilango choopsa m'banja lililonse, mwana woyamba kubadwa adzafa. ***(Eksodo 11: 4-6)*** Koma Farao sanakhulupirire kuti Mulungu adzachita kapena kubweretsa chilango choopsa chotere. ***(Eksodo 11: 10)***<br>• *Ife tikuyenera kuphunzira kuti chilichonse chimene Mulungu amayankhula kapena kunena m'Baibulo ndi choona ndipo chilichonse chimene amalonjeza, Iye adzachikwaniritsa.*<br>• Mulungu anafotokozera Mose zomwe Aisrayeli akuyenera kuchita kuti akonzekere kutuluka m'dziko la Aigupto. Banja lililonse linkayenera kupha mwanawankhosa. Iwo ankayenera kupaka magazi ake m'mbali mwa khomo la nyumba zawo pofuna kuonetsa kuti nyumbayo ndi ya Aisrayeli. Kenaka ankayenera kukhala ndi chakudya chapadera cha nyama ya nkhosa yootcha, buledi, ndi masamba owawa. Iwo ankayenera kudya mofulumira ndiponso atavala kukonzekera kuchoka msanga. Mulungu anafotokoza kuti Aisrayeli adzatetezedwa ngati pa khomo pa nyumba zawo pali magazi. ***(Eksodo 12: 12-13)***<br>• *Fotokozani za chisangalalo ndi chiyembekezo podziwa kuti tsopano akutuluka m'dzikomo komanso za m'mene Aisrayeli anatsatira malangizo onse. Kambiranani phindu ndi kufunika kwa magazi kwa Aisrayeli ndi momwe anakhalira chitetezo chawo.*<br>• *Sizapafupi kwa ife nthawi zonse kumvetsetsa machitidwe a Mulungu, koma titha kukhala ndi chitsimikizo kuti nthawi zonse amachita zabwino. Kodi Aisrayeli akanatetezedwa motani? M'njira yomweyo, aliyense amene amakhulupirira Ambuye Yesu kuti anafa pa mtanda amapulumutsidwa ku chilango chifukwa cha tchimo lathu. Baibulo limaphunzitsa kuti Ambuye Yesu ndi Mwanawankhosa wa Mulungu, osati wa Aisrayeli okha, koma dziko lapansi lonse kuphatikiza ife lero. Pamene takhulupirira magazi ake amene anakhetsa pamene anafa pa mtanda, tidzapulumutsidwa ku chilango cha machimo athu.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Mose ndi mliri wotsiriza. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Eksodo 12: 13***. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.<br>• Kodi ndi mawu ena ati amene tingagwiritse ntchito ponena za chilango cha Mulungu?<br>• Kodi chilango chomaliza pa Farao chidzakhala chotani?<br>• Kodi Aisrayeli ankayenera kuchita chiyani kuti atetezedwe?<br>• Kodi ankayenera kudya chiyani? Kodi ankayenera kudya motani?<br>• Kodi Mulungu anachita chiyani kuti ife tikhoza kupulumutsidwa? ***(Aroma 5: 8)*** |

## B10 Nkhani Yachitatu

## Mose ndi kuthawa ku Aigupto – Iyi ndi nkhani ya mphamvu yodabwitsa ya Mulungu.

**Ife tikuphunzira kuti:**

- Mulungu analanditsa Aisrayeli monga m'mene analonjezera pamene anayankhula ndi Mose pa chitsamba choyaka moto.
- Baibulo limafotokoza kuti ichi ndi chimodzi cha chitsanzo cha mphamvu yayikulu ya Mulungu.

**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 14: 30a***

**Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 12: 31-39; 14: 1-31***

**MAWU OYAMBA**

Tchulani zinthu zomwe ndi zovuta kwa ife kuzichita. Mwa chitsanzo: Kuyenda mlengalenga popanda kukwera ndege, kulowoka nyanja popanda bwato, ndi kuyenda m'chipululu popanda kalozera wa njira ndi zina zambiri. Koma zimene ndi zosatheka ndi anthu zimatheka ndi Mulungu. Mulungu anali pafupi kuonetsa mphamvu yake m'Baibulo.

**PHUNZITSANI**

- Nthawi ya usiku, pamene ana onse aamuna oyamba kubadwa a Aaigupto anafa, Farao anayitanitsa Mose ndi Aroni. *Kodi Farao ankachita chiyani m'mbuyomo kukachitika mliri? Fotokozani kusiyana kwake ndi nthawi iyi* - Iye anawawuza kuti atenge anthu onse pamodzi ndi ziweto zawo ndipo atuluke mu Aigupto nthawi yomweyo. ***(Eksodo 12: 31-32)*** Aaigupto anawalimbikitsanso kuti azipita chifukwa ankaopa kuti onse atha kufa ngati Aisrayeli apitirira kukhala pakati pawo.
- Iwo anawapatsa mphatso zasiliva, zagolide ndi zovala pamene ankachoka. ***(Eksodo 12: 35-36)*** Pa zonse, panali amuna 600,000 pamodzi ndi akazi ndi ana. *Ndi ana akulu msinkhu mutha kufanizira chiwerengero chimene ndi cha kudera kwanu.*
- Potsiriza Farao anamvera Mulungu! Iye akanapewa mavuto ngati akanamvera poyamba pomwe paja. *Panonso, tsindikani kufunika kwa kumvera makolo, aphunzitsi komanso kufunika komvera Mulungu!*
- Aisrayeli motsogozedwa ndi Mose analowera njira ya ku Nyanja Yofiira. *Kambiranani zomwe ankamva m'mitima mwawo.* Koma sikanali komaliza kuti aonenso Farao! Mulungu anawumitsanso mtima wa Farao; iye anayenera kuti aphunzire za ukulu wa Mulungu! Farao anazindikira kuti wataya anthu amene ankamangira nyumba zake ndipo anaganiza zowathamangira pa magaleta 600. ***(Eksodo 14: 3-7)***
- Aisrayeli anasowa kulowera! Farao anali kumbuyo kwawo ndipo Nyanja Yofiira inali kutsogolo kwawo. *Kodi mukuganiza kuti ankamva bwanji m'mitima mwawo? Fotokozani za mantha awo ndi za kutsutsana naye Mose.* Koma Mose anawawuza kuti asachite mantha koma ayime ndipo adzaona chipulumutso chimene Yehova adzawachitira! ***(Eksodo 14: 10-14)***
- Yehova anawuza Mose kuti anyamule ndodo yako ndi kutambasula dzanja lako kuloza ku nyanja. Mose anamvera ndipo modabwitsa njira inaoneka pakati pa Nyanja Yofiira kuti Aisrayeli onse anatha kuwoloka powuma.
- *Fotokozani zomwe zinachitika pamene Aaigupto anayamba kuwatsatira.* Mose anatukulanso ndodo ija ndipo madzi anabwerera. Baibulo limati ankhondo onse a Farao anamira m'madzi ndipo palibe amene anapulumuka. ***(Eksodo 14: 28)*** *Kodi inu mukanakhala Mwaisrayeli, mukanaganiza chiyani za Mulungu ameneyu? Fotokozani zomwe anachita ataona mphamvu yayikulu ya Mulungu - iwo anaopa Yehova (fotokozani) ndi kukhulupirira Iye komanso Mose.* ***(Eksodo 14: 31)***
- Ifenso, nthawi zonse titha kumakhulupirira Ambuye chifukwa cha mphamvu yake yayikulu. Monga Aisrayeli, tiyenera kukhulupirira Iye ndi kunena kuti, "Ambuye, pulumutseni INE!"

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Mose ndi kuthawa ku Aigupto.

**PHUNZIRANI**

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Eksodo 14: 30a***.

**KUMBUKIRANI**

Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.

- N'chifukwa chiyani Farao analola Aisrayeli kuti apite?
- Kodi Aaigupto anawapatsa chiyani?
- N'chifukwa chiyani Farao anasankha kuwathamangitsa?
- Kodi Farao anagwiritsa ntchito magaleta angati?
- N'chifukwa chiyani Aisrayeli anali ndi mantha kwambiri?
- Kodi Mulungu anawuza Mose kuti achite chiyani kuti apulumuke?
- Kodi chinachitika ndi chiyani kwa gulu la ankhondo la Aaigupto?
- Kodi Aisrayeli anachita chiyani ataona zomwe zinachitikazo?

## B10 Nkhani Yachinayi

**Mose ndi Israyeli ayamika Mulungu – Iyi ndi nkhani ya kuyamika Mulungu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Aisrayeli anali oyamika chifukwa cha zonse zimene Mulungu anachita powapatsa ufulu ndi chitetezo.<br>• Tonse tikuyenera kuyima ndi kuyang'ana m'mbuyo ndi kuyamika Mulungu chifukwa cha zimene watichitira m'miyoyo yathu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Salimo 106: 1***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 15: 1-22*** |
| **MAWU OYAMBA** | Gwiritsani ntchito mayankho a zinthu zodabwitsa zomwe zalembedwa m'Baibulo. Chitsanzo: Danieli kupulumuka m'dzenje la mikango, Davide kupha Goliate ndi zina zambiri kuphatikiza kuwoloka Nyanja Yofiira mu nkhani yathu ya sabata latha. Fotokozani kuti chilichonse cha izi, anthu a m'Baibulo anali ndi chochita chimodzi chokha ndiko kudalira mphamvu ya Mulungu. Tiona zomwe Aisrayeli anachita Mulungu atawapulumutsa ndipo muganize zomwe tikuyenera kuchita kwa Mulungu pa zomwe Iye amatichitira. |
| **PHUNZITSANI** | • Aisrayeli tsopano sanalinso akapolo koma afulu ndipo adani awo onse anali atamira m'madzi. *Fotokozani momwe ankamvera m'mitima mwawo.* Iwo ankadziwa kuti anali Mulungu amene anawapulumutsa, iwo anali oyamika ndipo anafuna kutamanda Mulungu pa zimene anachita. ***(Eksodo 15: 1)*** Iwo anazindikira ukulu wa Mulungu ndipo anayimba nyimbo yotamanda ukulu wake chifukwa anadziwa kuti palibe Mulungu wina amene ali ndi mphamvu ngati imeneyo. ***(Eksodo 15: 11)*** Iwo anayimba mozama zonse za zomwe anachita.<br>• *Ana akuyenera kuzindikira kuti Mulungu ndi wamkulu pa: 1) Chilengedwe. 2) Kukwaniritsa zosowa zathu zonse tsiku ndi tsiku. 3) Mwa chikondi chake chachikulu potumiza Mwana wake kuti adzafe pa mtanda chifukwa cha ife.*<br>• Aisrayeli sanangoyimba nyimbo kokha za Mulungu, koma anali ndi ubale wabwino ndiye motere iwo anati, "Mulungu wanga", "Mphamvu zanga", "Chipulumutso changa". ***(Eksodo 15: 2)***<br>• *Ana afunsidwe ngati akudziwa za Mulungu kokha kapena ali pa ubale wabwino ndi Iye ndipo amamudziwa ngati Atate awo a Kumwamba.*<br>• Aisrayeli sankangoganiza za nthawi imeneyo yokha, iwo ankadziwa kuti adzapitirira kuwathandiza pa nkhondo ndi adani awo pamene ali pa ulendo opita ku Dziko la Malonjezano. *Tiyeni tiphunzire kuti Ambuye sasintha ndipo titha kumudalira osati lero lokha koma nthawi zonse m'tsogolo.*<br>• Miriamu, mlongo wa Aroni, anatsogolera amayi kuyimba nyimbo ndi kuvina. Iwo anali osangalala pamene ankakondwerera zomwe Mulungu anachita.<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Mose ndi Israyeli ayamika Mulungu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Salimo 106: 1*** - Vesi iyi ikutikumbutsa za kuyamika Ambuye ndipo ana alimbikitsidwe kupemphera mapemphero oyamika zimene Ambuye anawachitira. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani kapena mukhale ndi mafunso ochokera pa B10.<br>• Kodi Aisrayeli anachita chiyani pamene anaona kuti tsopano ndi afulu?<br>• Kodi iwo anafotokoza kuti Mulungu ndi ndani wawo m'nyimbo yawo?<br>• Kodi Aisrayeli anadziwa chiyani za tsogolo lawo?<br>• Kodi ndi ndani anatsogolera amayi kuyimba ndi kuvina?<br>• Kodi mukuganiza ndi chifukwa chiyani Aisrayeli asintha kuchoka pa kukhala anthu amantha ndi kuyamba kuyimba nyimbo ndi kutamanda Mulungu? |

## <u>B11 Nkhani Yoyamba</u>

**Mulungu apereka chakudya – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kupereka chakudya kwa Aisrayeli.**

**Ife tikuphunzira kuti:**

- Mulungu anapereka chakudya kwa Aisrayeli kwa zaka makumi anayi m'chipululu.
- Ambuye Yesu ndi "Mkate Wamoyo" ndipo amakwaniritsa zosowa zathu.

**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 6: 35***
**Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 16: 1-32***

### MAWU OYAMBA

Kumbutsani ana mwachidule zomwe zinachitika mu B9 ndi B10. Mulungu anaonetsa Aisrayeli mphamvu yake powalanditsa m'dziko la Aigupto ndipo tsopano akulonjeza kuwatsogolera ku dziko latsopano.
Iwo asanayende mtunda wautali anthu anayamba kung'ung'udza ndi kudandaula kwa Mose za njala yawo! Chakudya chawo chinali chitatha, ndipo iwo anayamba kuganiza za kubwerera ku Aigupto ndi chakudya chonse ankadya kumeneko. ***(Eksodo 16: 2-3)*** Nthawi iyi anali atayiwala kale kuti Mulungu ndiye akulamulira ndi kuti ankadziwa za zosowa zawo zonse za pa ulendowu. *Ngati n'kotheka, mutha kukumbutsa ana kuti ili ndi khalidwe loyipali. Mulungu amafuna kuti tizimuyamika.*

### PHUNZITSANI

- Ngakhale anthu analephera kudalira Mulungu, Iye anaonetsa kuti amawasamalirabe. Mulungu anali ndi chikonzero choti azikhala ndi chakudya nthawi zonse. Iye ankayenera kutumiza chakudya kuchokera Kumwamba kuti azitenga m'mawa uliwonse. Pa tsiku lachisanu ndi chimodzi azitenga cha masiku awiri kuti azidya pa Sabata (tsiku lopatulika). Madzulo aliwonse azilandira nyama. ***(Eksodo 16: 4-12)***
- *Taganizani Aisrayeli akutuluka m'misasa yawo m'mawa ndipo fotokozani zomwe akuchita chifukwa cha zomwe apeza.* Mose anafotokoza kuti uwu ndi mkate umene Ambuye awapatsa. Aliyense ankayenera kutenga molingana ndi anthu amene anali mu msasa mwake. Palibe amene ankayenera kusunga wina kuti adzadye tsiku linalo. Anthu ena anayesera kusunga, koma pofika m'mawa tsiku linalo unali utaonongeka. ***(Eksodo 16: 15-20)*** *Tsindikani kufunika kochita zomwe Mulungu wanena m'malo mochita zomwe tikufuna.*
- Anthu anatchula mkate wa Kumwamba "Mana". Unkakoma ngati uchi! Mulungu anatumiza mana kwa Aisrayeli nthawi yonse anali pa ulendo. Mulungu anawapatsa maumboni okwanira kuti Iye anali Mulungu wawo ndi kuti adzawasamalira. ***(Eksodo 16: 31-32)***
- Mu nkhani yathu, Aisrayeli ankayenera kutenga ndi kudya mana kuti akhute. Ankawapatsa mphamvu za tsiku lililonse m'chipululu komabe ankayenera kudya mana tsiku ndi tsiku kuti akhale ndi moyo.
- *Patapita zaka zambiri, Yesu anabwera kuchokera Kumwamba kuti adzafe chifukwa cha machimo athu. Iye anazitcha "Mkate Wamoyo". Ngati mulandira Ambuye Yesu, (Mkate Wamoyo) m'miyoyo yanu, Iye amapereka moyo wosatha – moyo umene timasangalala nawo pa dziko lapansi ndipo Kumwamba. Mana wochokera Kumwamba chinali chodabwitsa chabwino kwa Aisrayeli koma tikalandira Ambuye Yesu timakhala ndi chinthu chopambana kwambiri. (Mutha kugawa magawo awiri pa pepala kuti ana amvetse bwino za mana ndi Mkate Wamoyo.)*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Mulungu apereka chakudya.

### PHUNZIRANI

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Yohane 6: 35***. Tsindikani ndi zomwe zili m'mwambazi.

### KUMBUKIRANI

Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.

- N'chifukwa chiyani anthu ankang'ung'udza?
- Kodi iwo ankadandaula kwa ndani?
- Kodi iwo ankayenera kuchita chiyani m'malo modandaula?
- Kodi mana ankapezeka kangati pansi pa sabata?
- Kodi madzulo aliwonse ankapeza chiyani?
- Kodi anatenga mana kwa nthawi yayitali bwanji?
- Kodi Yesu anadzitcha yekha kuti ndani?
- Kodi Yesu ndi woposa mana m'njira yanji?

**B11 Nkhani Yachiwiri**

**Mulungu apereka chipambano – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kuthandiza amene amamudalira.**

**Ife tikuphunzira kuti:**
- Mulungu anathandiza Aisrayeli pamene anamudalira.
- Mulungu amafuna kuti tizipemphera kwa Iye kuti tipambane m'miyoyo yathu.

**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 17: 15***
**Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 17: 8-15***

**MAWU OYAMBA**

Pasanapite nthawi Aisrayeli anakumana ndi vuto linanso. Gulu la ankhondo la adani otchedwa Amaleki anayamba kuwathira nkhondo. ***(Eksodo 17: 8)***
*Gwiritsani ntchito mafunso ali m'munsiwa kuti muchititse ana kuganiza za nyengo zawo:*
- *Kodi Aisrayeli ankayenera kuchita chiyani? (kumenyana nawo)*
- *Kodi ankazolowera kuchita nkhondo? Kumbutsani ana kuti ku Aigupto iwo anali akapolo osati asilikali.*
- *Kodi iwo anamva bwanji m'mitima mwawo?*
- *Kodi iwo akanadalira thandizo la Mulungu? Kumbutsani ana kuti Mulungu anawatulutsa m'dziko la Aigupto kuti apite nawo ku dziko latsopano. Iye anasunga lonjezo lake.*

**PHUNZITSANI**

- Mose anali mtsogoleri wanzeru ndipo ankadziwa zoyenera kuchita. Iye anapempha mthandizi wake Yoswa kuti asankhe asilikali. Mose anadziwa kuti asilikaliwa ankafuna thandizo la Mulungu, choncho iye anapita ndi Aroni ndi Huri pamwamba pa phiri loyang'anana ndi kumene amachita nkhondo. Mose ananyamula ndodo (kamtengo kakatali kamene abusa aziweto ankagwiritsa ntchito) ndi kuyikweza m'mwamba manja onse awiri. *Fotokozani kuti iyi inali njira yosonyeza kuti Aisrayeli akudalira Mulungu kuti awathandiza kupambana.* ***(Eksodo 17: 9)***
- Mose ankati akamachita zimenezi, Aisrayeli ankapambana. *Funsani ana kuti akweza manja awo pamwamba pa mitu yawo. Kodi mukuganiza chingachitike ndi chiyani ngati mutakweza manja anu nthawi yayitali?* Pasanapite nthawi manja a Mose anatopa ndipo anawatsitsa. Pamenepo adani anayamba kupambana. *Funsani ana aganize zomwe Aroni ndi Huri akanachita kuti athandize Mose, kenaka mufotokoze zomwe zinachitika.* Kenaka Mose anatukula manja ake mpaka pamene dzuwa linkalowa ndipo nthawi imeneyo Aisrayeli anapambana. Mose ankafuna kuthokoza Mulungu chifukwa cha chipambano, motero anamanga guwa la miyala ndipo analitcha "Yehova Chipambano Changa". *Fotokozani kuti Mose ankafuna kuti Mulungu alandire ulemu onse chifukwa cha chipambano.* ***(Eksodo 17: 10-13, 15)***
- *Kodi inu mukuganiza kuti ndi ndani amene anatenga gawo lalikulu pa chipambano chawo pa nkhondo? Yoswa ndi asilikali sakanatha okha kupambana Mose akanapanda kukweza manja ake kwa Mulungu ndi kumudalira. Ngati takhulupirira Ambuye Yesu kukhala Mpulumutsi wathu, tilinso ndi m'dani – Satana. Iye amafuna kutichititsa mantha ndi kutichotsera chimwemwe m'miyoyo yathu. Kodi ali ndi mphamvu zambiri ndi Ambuye Yesu kapena Satana? Pakuti Yesu ndi wamphamvu kwambiri, ife titha kupambana. Ife tikuyenera kumudalira Iye.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Mulungu apereka chipambano.

**PHUNZIRANI**

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Eksodo 17: 15.***

**KUMBUKIRANI**

Ana apange chikwangwani chachikulu ndipo alembe ndi kukongoletsa mawu akuti, "Yehova Chipambano Changa."
Kapena mutha kugwiritsa ntchito mafunso awa:
- Kodi mtsogoleri wa asilikali wa Aisrayeli anali ndani?
- Kodi Mose anapita kuti?
- Kodi ndi ndani anapita ndi Mose?
- Kodi chinkachitika ndi chiyani mu nkhondo Mose akakweza manja ake?
- Kodi Mose ananyamula manja ake mpaka nthawi yanji?
- Kodi anawapambanitsa ndani?
- Kodi m'dani wathu ndi ndani?
- Kodi ife tikuyenera kudalira ndani kuti atithandize?

<u>**B11 Nkhani Yachitatu**</u>

**Mulungu apereka malamulo – Iyi ndi nkhani ya malamulo a Mulungu.**

**Ife tikuphunzira kuti:**
- Mulungu ndi woyera.
- Ife sitingathe kusunga malamulo a Mulungu.

**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 20: 1 kapena Aroma 3: 23***
**Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 19-20***

**MAWU OYAMBA**

Fotokozani za malamulo amene muli nawo pa sukulu kapena pa nyumba. Kodi ndi ati? N'chifukwa chiyani timakhala ndi malamulo? Kodi nthawi zonse n'kosavuta kumvera malamulo? M'phunziro lathu lero tiphunzira momwe Mulungu anaperekera malamulo kwa Aisrayeli.

**PHUNZITSANI**

- Aisrayeli anafika pa phiri lalikulu lotchedwa Sinai pamene anamanga misasa yawo. Mulungu anawuza Mose kuti atsika mu mtambo ndi kukhala pamwamba pa phiri. Mose ayike chizindikiro cha miyala m'tsinde kuzungulira phirilo kuti munthu aliyense asakwere. Ngakhale anthu anasamba ndi kudzikonzekeretsa, tchimo lawo linawalepheretsa kufika kufupi ndi Mulungu. ***(Eksodo 19: 1-14)***
- Pa tsiku lachitatu anthu anayimirira mu tsinde la phiri. Utsi unkatuluka m'phiri ndipo phiri linagwedezeka. *Fotokozani kuti izi zinkasonyeza kuti Mulungu ndi wamphamvu kwambiri.* Kambiranani momwe anthu ankamvera m'mitima mwawo. Kenaka Mulungu anayitana Mose kuti akwere phiri ndipo Mulungu anawuza Mose kachiwiri kuti achenjeze anthu akhale mu tsinde la phiri. ***(Eksodo 19: 16-22)*** *Fotokozani kuti anthu sakanatha kufika pafupi ndi Mulungu chifukwa Iye ndi woyera (wopanda tchimo) koma iwo anali ndi machimo m'miyoyo yawo. Lero, tchimo limatilekanitsabe ndi Mulungu pokhapokha ngati machimo athu akhululukidwa.*
- Kenaka Mose analandira malamulo khumi atalembedwa pa miyala. Malamulo anali malangizo a Mulungu ndipo anafotokoza momwe anthu a Mulungu akuyenera kukhalira moyo wawo. Iwo ankayenera kukonda Mulungu kuposa wina aliyense ndiponso ankayenera kukondana wina ndi mnzake. *Kwa ana a Kalasi 2 zitha kukhala bwino kuwerenga ndime imeneyi ndi kufotokoza lamulo lililonse mwachidule. Mufotokoze kuti lamulo 1 mpaka 4 akunena za ubale wathu ndi Mulungu ndipo lamulo 5 mpaka 10 akufotokoza za ubale wathu ndi anthu ena. Athandizeni ana kuti amvetse kuti ife talephera kumvera malamulo amenewa!* ***(Eksodo 20: 1-17)***
- *Mwachisoni, Aisrayeli sanathe kusunga malamulo a Mulungu komanso ngakhale ife. Tonse timalephera kukwaniritsa zomwe Mulungu amayembekezera kuchokera kwa ife. Ife ndife ochimwa. Ndi Ambuye Yesu okha amene anakhala moyo wangwiro pa dziko lapansi. N'chifukwa chake Iye ndiye Mpulumutsi wathu. Iye anafa kuti alangidwe m'malo mwathu chifukwa cha machimo athu, kuti Mulungu atikhululukire. Pamenepo ife tidzakhala anthu a m'banja la Mulungu ndipo sitidzakhala kutali monga anachitira Aisrayeli.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Mulungu apereka malamulo.

**PHUNZIRANI**

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Eksodo 20: 1*** kapena ***Aroma 3: 23***.

**KUMBUKIRANI**

Pa mafunso mutha kukhazikika pa malamulo enieniwo monga m'mene alembera mu phunziro la Kalasi 2. Ngati n'kotheka lembani pa bolodi kapena chipepala kuti ana azitha kuona ndi kumva. Mukamaliza kuwerenga onse, chotsani kapena fufutani. Musiye mawu oyamba a lamulo, monga: Usakhale ndi ______ ina koma Ine ndekha. Usadzipangire _______chinthu chilichonse. Ngati mwana wina akudziwa mawu amene palibewo, atha kulandira poyinti a gulu lawo.
Ana aang'ono atha kuwumba kapena kupanga Phiri la Sinai. Iwo akapanga, mutenge thonje ndi kuyika pamwamba kusonyeza mtambo ndiponso muyike zofiira kusonyeza moto kenaka mulembe mizere yokhotakhota kuyimira mabingu ndi zing'aning'ani. Ikani mpanda kuzungulira chomwe apanga. Ana aonjezere timisasa m'mbali mwake.

## <u>B11 Nkhani Yachinayi</u>

**Mulungu apereka chipulumutso – Iyi ndi nkhani ya njira ya Mulungu yopulumutsira anthu ku imfa.**

**Ife tikuphunzira kuti:**
- Mulungu anapereka njira kwa Aisrayeli yothawira chilango chowayenera.
- Mulungu anapereka njira yoti ife tipulumukire.

**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 3: 14***
**Ndime Yowerenga:** ***Numeri 21: 4-9***

### MAWU OYAMBA

Nthawi zina timabwereza cholakwa chomwecho! Kodi mungakumbukire zomwe Aisrayeli anachita pamene chakudya anatenga ku Aigupto chitatha? Inde, anang’ung’udza ndi kudandaula! Ndipo mu nkhani ya lero akung’ung’udzanso! Tiyeni tione chifukwa chake.
Kapena
Yankhulani za kuopsa kolumidwa ndi njoka, kufunika kopita ku chipatala ndi kulandira mankhwala. Mu nkhani ya lero Mulungu anali ndi mankhwala osiyana kwambiri ofuna kuchizira amene alumidwawo.

### PHUNZITSANI

- Mwachisoni, Aisrayeli anayankhula motsutsana ndi Mose ndi Mulungu ponena kuti zikanakhala bwino akanawasiya ku Aigupto kuja ndipo sankakonda mana amene Mulungu ankawapatsa. Taonani anthu osayamika awa! ***(Numeri 21: 5)***
- Nthawi iyi Mulungu anakwiya ndi anthuwo ndipo anaganiza zowalanga. Mosachedwa m’misasa munabwera njoka zaululu kwambiri. *Kodi chinkachitika kwa anthu ndi chiyani?* Inde, anthu ankalumidwa ndipo ambiri anafa. Nthawi yomweyo anthu anazindikira kulakwa kwawo. Iwo anabwera kwa Mose kumuwuza kuti anachimwa ndi kumupempha kuti apemphere kwa Mulungu kuti achotse njokazo. ***(Numeri 21: 6-7)*** *Thandizani ana kuti azindikire kuti umenewo ndi moyo woyenera pamene tachita cholakwa. Tikuyenera kuvomereza tchimo lathu ndi kupempha Mulungu kuti atithandize.*
- Mose atapemphera kwa Mulungu, Mulungu anawuza Mose kuti achite chinthu chachilendo. Iye ankayenera kupanga njoka yamkuwa ndi kuyipachika pa mtengo pakati pa misasa. Njoka yamkuwayo inali pamalo poti aliyense atha kuyiona. Mulungu analonjeza kuti aliyense amene walumidwa sadzafa akadzayang’ana njokayo pa mtengopo. Aliyense amene anakhulupirira zimenezi ndi kuchita zomwe Mulungu ananena, anakhala ndi moyo! ***(Numeri 21: 8-9)*** *(Ngati mwatsatira langizo lachiwiri pa mawu oyamba aja, mutha kufananitsa.) Kodi mukuganiza kuti Aisrayeli anamvera malangizo a Mulungu? Chifukwa chiyani? Tsindikani kuti iyi inali njira yokhayo yoti akhale ndi moyo – zinali zopanda phindu kutsatira njira zina!*
- Patapita zaka, pamene Yesu anabwera pa dziko lapansi, Iye anagwiritsa ntchito nkhani iyi pophunzitsa aliyense phunziro lofunika kwambiri. Ife tili ngati Aisrayeli chifukwa tinachimwira Mulungu ndipo tidzalangidwa chifukwa cha machimo athu. Koma Mulungu anapereka njira yoti ife tipulumukire ku chilango chifukwa cha machimo athu. Yesu anafotokoza kuti Iye “adzapachikidwa” pamene adzafa chifukwa cha machimo athu. Ife tikakhulupirira zimene Yesu anatichitira, Mulungu amatipulumutsa ndi kutipatsa moyo wosatha. *Tsindikani kuti ndi kudzera mwa Yesu yekha pamene tingapulumutsidwe ndipo limbikitsani ana kuti achite chisankho chimenechi.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Kuonetsa:** Onani FBI Zoonjezera C – Mulungu apereka chipulumutso.

### PHUNZIRANI

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n’koyenera Vesi Yoloweza: ***Yohane 3: 14***. Awuzeni kuti awa ndi mawu a Yesu. Iye anafotokoza momwe adzatipulumutsire pamene adzapachikidwa pa mtanda.

### KUMBUKIRANI

Kagulu ka ana katha kupanga chidole cha njoka yamkuwa ndi kuyipachika pa mtengo ndipo kagulu kena kapange mtanda. Vesi Yoloweza ilembedwe pa zimene anawo apanga.
Kapena ana apange njoka za dongo ndi kuzikungiza pa pensulo ngati pa mtengo.
Kapena muwafunse mafunso kuchokera mu nkhani zonse za mu B11.
Nawa mafunso ena owonjezera mu B11:
- Kodi nthawi iyi Aisrayeli ankadandaula chiyani?
- Kodi Mulungu anawalanga motani?
- Kodi anthu ankayenera kuchita chiyani kuti achiritsidwe akalumidwa ndi njoka?
- Kodi tingapulumutsidwe bwanji ku chilango cha machimo athu?

**B12 Nkhani Yoyamba**

**Yosefe ndi mngelo – Iyi ndi nkhani ya Yosefe kumvera Mulungu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Dzina loti ‘Yesu’ limatanthauza ‘Mpulumutsi’.<br>• Monga Yosefe, ife tiyenera nthawi zonse kumvetsera ndi kumvera Mulungu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 1: 21***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Mateyu 1: 18-25*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za mayina ndi matanthauzo ake – Funsani ana ngati akudziwa matanthauzo a mayina awo kapena chifukwa chomwe anawatchula mayina amenewo.<br><br>Fotokozani kuti ana lero aphunzira za mwana wapadera kwambiri m’Baibulo amene anapatsidwa dzina lapadera kwambiri. Lolani ana aganizire kuti nkhani imeneyi ndi ya ndani. |
| **PHUNZITSANI** | • Yosefe ndi Mariya ankakonzekera zokwatirana, koma tsiku lina Mariya anawuza Yosefe kuti anali woyembekezera. Yosefe anadziwa kuti iye sanali bambo a mwanayo motero anaganiza zoti asakwatirenso Mariya. ***(Mateyu 1: 18-19)***<br>• Usiku wina Yosefe anali ndi maloto. Mngelo anamuonekera m’maloto ndi kuyankhula naye. Mngelo anati, “Usaope kumutenga Mariya kukhala mkazi wako, chifukwa mwana akuyembekezerayo ndi wochokera kwa Mzimu Woyera.” ***(Mateyu 1: 20)*** *Fotokozerani ana kuti izi zikutanthauza kuti mwanayo ndi Mwana wa Mulungu.*<br>• Mngelo anawuza Yosefe kuti amupatse mwanayo dzina loti ‘Yesu’ chifukwa adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo. ***(Mateyu 1: 21)*** Fotokozani kuti dzina loti Yesu limatanthauza “Mpulumutsi”. *Kambiranani chomwe mpulumutsi ali (chitsanzo cha tsiku ndi tsiku: munthu amene akumira m’madzi amafunika mpulumutsi). Fotokozerani ana za ntchito ya ‘Yesu’ monga Mpulumutsi. Baibulo limanena kuti aliyense akufunika kupulumutsidwa ku chilango cha tchimo - Yesu sanachite tchimo choncho anali woyenera kulandira chilango cha tchimo la dziko lonse pamene anafa pa mtanda. Baibulo limanena kuti munthu aliyense akuyenera kumva chisoni chifukwa cha tchimo lake ndi kulola kuti Yesu akhale Mpulumutsi wake.*<br>• Yosefe atadzuka ku maloto ake, anachita zomwe anawuzidwa ndipo anakwatira Mariya. Patapita nthawi mwana anabadwa, ndipo Yosefe ndi Mariya anamutcha ‘Yesu’. ***(Mateyu 1: 24-25)*** Funsani za malangizo amene Yosefe anawuzidwa ndi kukambirana momwe iwo anachitira. Fotokozani kufunika kwa kumvera malangizo a Mulungu amene ali m’Baibulo ndi kuwatsatira. Pamodzi, ganizani ndi kulemba malangizo ena amene Mulungu anatipatsa kuti tiwatsatire.<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Yosefe ndi mngelo. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n’koyenera Vesi Yoloweza: ***Mateyu 1: 21***. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.<br>• Kodi Yosefe ankafuna kukwatira ndani?<br>• Kodi Mariya anawuza nkhani yotani Yosefe?<br>• Kodi Mulungu anayankhula kwa Yosefe m’njira yanji?<br>• Kodi Atate a mwanayo anali ndani?<br>• Kodi mwanayo adzatchedwa ndani?<br>• Kodi dzina loti ‘Yesu’ limatanthauza chiyani?<br>• Kodi Yosefe anachita chiyani atadzuka atalota?<br>• Kodi tikuyenera kupulumutsidwa ku chiyani? |

## B12 Nkhani Yachiwiri

**Herode ndi anzeru a kum'mawa – Iyi ndi nkhani ya anzeru a kum'mawa kufuna kupeza Yesu.**

**Ife tikuphunzira kuti:**
- Yesu ndi Mfumu ya mafumu.
- Yesu akuyenera kupembedzedwa.

**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 2: 2***
**Ndime Yowerenga:** ***Mateyu 2: 1-8***

### MAWU OYAMBA

Funsani ana atchule mayina a anthu ofunika kwambiri. Lembani mayinawo kapena mukhale ndi zithunzi zawo.
Kukambirana – Kodi mungakonde mutakumana ndi anthu amenewa? Ngati mungakonde mudzanena chiyani kwa iwo? Mudzichita chiyani? Mudzachita chiyani kwa iwo?
Uzani ana kuti lero muphunzira za anthu ena amene anayenda ulendo kukafuna munthu wofunika kwambiri kuposa wina aliyense anakhalapo.

### PHUNZITSANI

- Tsiku lina anzeru a kum'mawa amene ankakhala kutali kwambiri ndi kumene Yesu anabadwira anaona nyenyezi mlengalenga. *Fotokozani za kusangalala kwawo pamene anazindikira tanthauzo lake. Fotokozani momwe anayendera kuchokera kum'mawa pa ulendo wautali (miyezi!) mpaka kufika ku nyumba yaufumu ya Mfumu Herode.* Fotokozani zomwe iwo ananena kwa Mfumu Herode. "Ali kuti amene wabadwa kukhala Mfumu ya Ayuda? Chifukwa tinaona nyenyezi yake kum'mawa ndipo tabwera kudzamupembedza." ***(Mateyu 2: 1-2)*** *Fotokozani kwa ana kuti Mfumu yatsopano imene inkayenera kubadwa anali Yesu, Mwana wa Mulungu, ndi kuti Iye adzakhala wamkulu kuposa mfumu ina iliyonse inakhalapo. Yesu ndi Mfumu ya Mafumu. Funsani ana ngati akukumbukira tanthauzo la dzina la Yesu kuchokera m'phunziro la m'mbuyo. Kambiranani zomwe anzeru a kum'mawa ankatanthauza pamene anati iwo ankafuna 'kupembedza' Mfumu. N'chifukwa chiyani Yesu anali woyenera kupembedzedwa?*
- Pamene Herode anamva za Mfumu yatsopano, anali ndi nkhawa kwambiri. Iye sankafuna wina aliyense kutenga malo ake ngati mfumu. Iye anayitana alangizi ake ena ndipo anawafunsa za kumene Mfumu yatsopano ikuyenera kubadwira. Iwo anafufuza m'Malemba ndipo anapeza kuti mwanayo adzabadwira ku mzinda wotchedwa Betelehemu. ***(Mateyu 2: 3-6)***
- Herode anayitana anzeru a kum'mawa aja ndipo anati, "Pitani mukafufuze za mwanayo mosamalitsa. Ndipo mukamupeza mudzandiwuze kuti inenso ndikamupembedze." ***(Mateyu 2: 7-8)*** *Fotokozani kuti Herode sankafuna kukapembedza Mfumu yatsopano, iye ankafuna kukapha Mfumuyo. Funsani ana zomwe akuganiza kuti ndi chifukwa chomwe Herode ankafuna kuphera Mfumu yatsopanoyo. Fotokozani kuti anthu ambiri lero sasamala za Yesu monga m'mene akuyenera kuchitira, koma Mulungu akufuna kuti ife timukonde ndi kumupembedza monga anachitira anzeru a kum'mawa.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Herode ndi anzeru a kum'mawa.

### PHUNZIRANI

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Mateyu 2: 2***.

### KUMBUKIRANI

Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.
- Kodi chinachitika ndi chiyani mlengalenga?
- Kodi anthu anzeruwa anachokera kuti?
- Kodi iwo anapita kuti kukafuna Mfumu yatsopano?
- Kodi Mfumu imene anayankhula nayo dzina lake linali ndani?
- Kodi Mfumu Herode anamva chiyani mu mtima mwake pamene anamva za Mfumu yatsopano?
- Kodi iwo anapeza kuti Mfumuyo inkayenera kubadwira mu mzinda uti?
- Kodi Herode anawuza anzeru a kum'mawa kuti achite chiyani?
- Kodi wamkulu kuposa mafumu onse ndi ndani?

## B12 Nkhani Yachitatu

**Anzeru a kum'mawa ndi Yesu – Iyi ndi nkhani ya anzeru a kum'mawa kutsatira nyenyezi ndi kupeza Yesu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Anzeru a kum'mawa anapembedza Yesu ndi kumupatsa mphatso zapadera kwambiri.<br>• Ife titha kupembedza Yesu lero.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 2: 11***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Mateyu 2: 9-12*** |
| **MAWU OYAMBA** | Kukambirana – Kodi ndi mphatso yotani yopambana imene munapatsidwa? (Ana atha kujambula mphatsoyo.) Ngati mukukaona mwana watsopano kodi mungatenge mphatso yanji?<br><br>Fotokozerani ana kuti lero tiphunzira za mphatso zimene anzeru a kum'mawa anapereka. Funsani ana afotokoze zomwe anaphunzira za anzeru a kum'mawa m'phunziro la sabata latha. |
| **PHUNZITSANI** | • Anzeru a kum'mawa anachoka pamaso pa Herode ndi kupita. Iwo anaonanso nyenyezi ija ndipo inawatsogolera ku malo kumene kunali Yesu. ***(Mateyu 2: 9-10)*** *Kambiranani zomwe anzeru a kum'mawa anamva mu mtima mwawo pamene anaona nyenyezi ija. N'chifukwa chiyani anamva motero?*<br>• Anzeru a kum'mawa anafika pa nyumba ina ku Betelehemu m'mene mukhala Yosefe ndi Mariya ndi mwana Yesu. Iwo analowa ndipo ataona Yesu anagwada ndi kumupembedza. Iwo anamupatsa mphatso zitatu: golide, lubani (ochokera ku khungwa la mtengo onunkhira), ndi mure (izi zinkachokera ku kamtengo ka minga konunkhira kapena ka mankhwala). ***(Mateyu 2: 11)***<br>• *Funsani ana ngati mphatso zimenezi ndi zimene iwo akanapereka kwa mwana wankhanda. Fotokozani kuti mphatso izi zinali za mtengo wapatali kwambiri ndipo zinkaperekedwa kwa Mfumu yekha basi. Kambiranani – mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani anzeru a kum'mawa anasankha mphatso zimenezi kuti apereka kwa khanda Yesu? Fotokozani kuti ngakhale ife sitingapereka mphatso ngati anzeru a kum'mawa, koma titha kupembedza Mulungu poyamika chifukwa cha zinthu zonse zimene amatichitira komanso ngati njira yokondweretsa Iye.*<br>• Patapita nthawi pang'ono, inali nthawi yoti anzeru a kum'mawa azipita kwawo. Herode anawapempha kuti akabwerenso kwa iye kuti adzamuwuze kumene kuli mwanayo, koma Mulungu anawachenjeza m'maloto kuti asapitenso kwa Herode, choncho iwo anadzera njira ina. ***(Mateyu 2:12)***<br>*Kukambirana – Kodi mukuganiza anzeru a kum'mawa aja anamva bwanji m'mitima mwawo pamene ankapita kwawo? Kodi mukuganiza kuti anawuza anthu chiyani atafika kwawo?*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Anzeru a kum'mawa ndi Yesu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Mateyu 2: 11.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.<br>• Kodi anzeru a kum'mawa anaonanso chiyani mlengalenga?<br>• Kodi anamva bwanji mu mtima pamene anaonanso nyenyezi ija?<br>• Kodi nyenyezi inawatsogolera kuti?<br>• Kodi m'nyumbamo munali ndani?<br>• Kodi anzeru a kum'mawa anachita chiyani ataona Yesu?<br>• Kodi iwo anamupatsa mphatso zingati?<br>• Tchulani mphatso imodzi.<br>• Kodi anzeru a kum'mawa anadziwa bwanji kuti akuyenera kudzera njira ina akamapita kwawo? |

## B12 Nkhani Yachinayi

**Kuthawira ku Aigupto – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kusamalira Mwana wake.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Mulungu anateteza Mwana wake.<br>• Ife tikuyenera kumvera Mulungu monga anachitira Yesu, Mariya ndi Yosefe.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 2: 15***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Mateyu 2: 13-23*** |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ana akuwuzeni maloto amene analota nthawi ina.<br>Kumbutsani kuti maloto a m'Baibulo nthawi zambiri ankakhala ndi matanthauzo apadera. Afunseni akuuzeni maloto amene aphunzira mpaka pano mu nkhani (maloto a Yosefe, maloto a anzeru a kum'mawa).<br>Lero tiphunziranso za maloto ena. |
| **PHUNZITSANI** | • Anzeru a kum'mawa atapita kwawo, Yosefe analota maloto. M'maloto amenewa Mulungu anawuza Yosefe kuti Herode wakwiya kwambiri ndipo akufuna kupha Yesu. Mulungu anawuza Yosefe kuti ankayenera kutenga Yesu ndi Mariya ndi kuthawira ku Aigupto kuti akatetezedwe. ***(Mateyu 2: 13)*** *Kambiranani - Kodi mukuganiza Yosefe anamva bwanji mu mtima mwake pamene analota maloto amenewa?*<br>• Usiku omwewo Yosefe anachita zimene anawuzidwa ndipo anatenga banja lake ndi kupita nalo ku Aigupto. Iwo anakhala kumeneko kwa nthawi mpaka pamene anamva kuti Mfumu Herode wamwalira. ***(Mateyu 2: 14-15)*** *Kambiranani - Kodi mukuganiza chikanachitika ndi chiyani ngati Yosefe akanapanda kuchita zomwe Mulungu anamuwuza m'maloto? Kunali kofunika kuti Yosefe achite zomwe Mulungu anamuwuza. Funsani ana kuti aganize kuti zotsatira zake zikanakhala zotani. Kambiranani kuti iwo sankayenera kuchita mantha.*<br>• *Mulungu anafunsa anthu, otchedwa aneneri, kuti alembe za kubadwa kwa Yesu zaka zambiri m'mbuyomo Iye asanabadwe. Mmodzi mwa aneneriwo anali Hoseya. Buku lake lili m'Chipangano Chakale. Iye analemba za Yesu ali ku Aigupto.*<br>• *Fotokozani momwe Vesi Yoloweza ikuyankhulira za Yesu ali ku Aigupto – Mulungu anadziwa zomwe Herode ankafuna kuchita zinthuzo zisanachitike. Pa chilichonse chomwe chinachitika, Mulungu ankateteza Mwana wake.*<br>• Pamene Herode anamwalira mngelo wina anabwera kudzamuwuza Yosefe kuti abwerere ku Israyeli. Apanso Yosefe anamvera. *Tsindikani kuti Mulungu ndiye ankalamulira zonse ndi kuteteza.*<br>• Yosefe, Mariya ndi Yesu anabwerera ndi kukakhala ku mzinda wa Nazarete. ***(Mateyu 2: 19-23)*** *Uzani ana kuti pamene Yesu ankakula ku Nazarete, Iye nthawi zonse ankamvera makolo ake, anansi ake, ndi, kuposa onse, ankamvera Atate ake Mulungu.* ***(Luka 2: 52)*** *Kumbutsani ana kuti Mulungu amafuna tizichita zinthu zimene zimamukondweretsa. Chinthu chabwino chomukondweretsa chomwe tingachite ndi kumuyamika chifukwa chotumiza Yesu kudzakhala Mpulumutsi wathu ndi kumupempha kuti atikhululukire machimo athu.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kuthawira ku Aigupto. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Mateyu 2: 15***. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani.<br>• Kodi chinachitika ndi chiyani kwa Yosefe anzeru a kum'mawa atachoka?<br>• Kodi Mulungu anawuza Yosefe kuti apite kuti?<br>• N'chifukwa chiyani ankayenera kupita kumeneko?<br>• Kodi Yosefe anatenga ndani pamene ankapita ku Aigupto?<br>• Kodi anabwerera kwawo liti?<br>• Kodi iwo anapita ku mzinda uti kukakhala?<br>• Kodi Yesu ankakhala moyo wotani pamene ankakula ku Nazarete?<br>• Kodi ife tingachite chiyani kuti tikondweretse Mulungu? |

# Malangizo a Aphunzitsi a Kachongedwe ka Maphunziro

**Maphunziro a Kalasi Yoyamba**
- Sabata lililonse pali masamba anayi amene akufunika kuchekenira ndi kulembamo mawu pang'ono.
- Sabata lililonse pali marikisi 20 amene akuyenera kuperekedwa kuchokera pa marikisi 80 a mwezi onse.
- Ana amene akuphunzira maphunziro a Kalasi Yoyamba iwo sakuyenera kuwerenga chifukwa sangathe kuwerenga bwino ndipo tikuyembekezera makolo/owang'anira/atsogoleri awo kuwathandiza.

**Maphunziro a Kalasi Yachiwiri**
- M'buku muli maphunziro anayi pa sabata.
- M'phunziro lililonse muli nkhani. Ophunzira akuyenera kupeza mawu osiyanasiyana m'phunziro, ndi kuchekenira, kutsiriza Mavesi Oloweza ndi zina zambiri.
- Sabata lililonse pali marikisi 20 pa marikisi 80 a mwezi uliwonse pamene atsiriza maphunziro onse molondola.

**FUNDO ZA KACHONGEDWE**

Choyamba aphunzitsi akupemphedwa kuti:
- Onani phunziro lililonse ndipo chongani moyenera zolondola kapena zolakwitsa.
- Perekani marikisi amene mwalangizidwa kutero.
- Nthawi zonse chongani pogwiritsa ntchito mitundu yosiyana ya zolembera, CHONGANI yankho lolondola.
- Lembani yankho lolondola poyenera kutero ndi kukonza mawu olakwika kalembedwe ake, koma MUSACHOTSE marikisi.
- Perekani marikisi ochepa pa yankho lolondola mbali imodzi yokha.
- Phatikizani marikisi onse a pa mwezi ndipo lembani kumapeto pa malo amene mwapatsidwa.

N'kofunika kusaumira ndi kuchita chilichonse chothandiza kulimbikitsa ophunzira kuti aphunzire Baibulo lawo. N'zothandizanso kuti kumapeto kwa mwezi uliwonse mphunzitsi azilemba mawu a chilimbikitso kwa wophunzira pa malo amene aperekedwa. Mutha kulemba ndemanga yoyamikira kuchekenira bwino, zilembo zabwino ndi kumvetsa bwino phunziro ndi zina zambiri.

Yesetsani kuti ndemanga, mafunso, ziganizo, zomwe mwaona ndi zina zambiri zikhale zosiyanasiyana, kuti zithandize kupanga zinthu kukhala zosiyana. Izi zimafunika kuganiza bwino, ndipo ndi kofunika kuti wophunzira azikhala ndi chidwi nthawi zonse. Ngati chiganizo chomwecho kapena funso lomwe likubwera mwezi uliwonse, zimachotsa chidwi cha wophunzira.

**Kalasi Yoyamba**
**Ndemanga zina**
"Chikondi – Ine ndasangalala kuti inu mwayamba maphunziro awa ndipo ndikukhulupirira kuti muwakonda. Zochekenira zanu ndazikonda. Kodi mumapita ku sukulu? Ndikuyembekezera kumva kuchokera kwa inu posachedwa."
"Wachita bwino, Andreya. Wachekenira bwino kwambiri! Kodi zimavuta pamene mumachekenira mizere ya m'kati? Inu musiyako zochepa zokha munachekenira pang'ono phunziro lapita lija."

**Ndemanga zauzimu**
"Wachita bwino, Sarah. Yairo analitu munthu wokondwa kwambiri pamene Yesu anamuthandiza."
"Yankho labwino kwambiri! Nkhani ya kufa kwa Yesu ndi yomvetsa chisoni, koma chokondweretsa ndi chakuti Iye anaukanso."

**Kalasi Yachiwiri**
**Ndemanga zina**
"Yankho labwino, Chimwemwe – Ine ndikukhulupirira kuti aphunzitsi ako akusangalala kwambiri ndi ntchito yako ku sukulu!"
"Ine ndikudziwa kuti posachedwapa ndi tsiku lako lobadwa, Chisomo. Kodi udzachita phwando? Udzachitira kuti? Udzakhale ndi tsiku lopambana kwambiri!"
"Iwe wayesetsa kwambiri. Pali zolakwika zochepa chabe. Usamayiwale kuonanso mayankho nthawi iliyonse."

**Ndemanga zauzimu**
"Ine ndasangalala ndi mmene wachekenira chithunzi cha Yesu ali nkhanda modyera ng'ombe. Kodi sizinali zabwino kuti Mulungu atumize Mwana wake ku dziko lapansi kwa ife?"
"Mitundu yako ndayikonda kwambiri! Zakariya anapereka dipo chifukwa cha kusakhulupirira zimene Mulungu ananena. Iye anakayikiranso Mawu a Mulungu."
"Mayankho abwino kwambiri. Munthu amene anakumana ndi Filipo ku chipululu anapita kwawo akusangalala kwambiri. Iye anamva ndi kukhulupirira nkhani yabwino ya Yesu."

| Zoonjezera A - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m'Chithunzi** |
| **B7** | **Yosefe** | **Kuyamika m'Nyumba ya Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-joseph-brothers/ |
| | | **Benjamini ndi nkhani yoyipa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-joseph-reunion/ |
| | | **Kukhululuka ndi nkhani yabwino** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-joseph-reunion/ |
| | | **Onse pamodzi mu Aigupto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-joseph-reunion/ |
| | | |
| **B8** | **Anthu amene Yesu** | **Anthu amene Yesu anakumana nawo - Mayi wodwala** |
| | **anakumana nawo** | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-024-peter-mother-in-law/ |
| | | **Anthu amene Yesu anakumana nawo - Munthu wakhate** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-025-jesus-leper/ |
| | | **Anthu amene Yesu anakumana nawo - Munthu wosowa thandizo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-jesus-lame-man/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/btbm-lame-man/ |
| | | **Anthu amene Yesu anakumana nawo - Mateyu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-027-matthew/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-zacchaeus-preschool/ |

| Zoonjezera A - Kalasi Yachiwiri Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m'Chithunzi** |
| **B7** | **Yosefe** | **Kufika kwa abale a Yosefe** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-brothers-1/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-joseph-brothers/ |
| | | **Benjamini ndi nkhani yoyipa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-joseph-reunion/ |
| | | **Kukhululuka ndi nkhani yabwino** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-joseph-reunion/ |
| | | **Onse pamodzi mu Aigupto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-reunion/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/joseph-jacob/ |
| | | |
| **B8** | **Anthu amene Yesu** | **Anthu amene Yesu anakumana nawo - Mayi wodwala** |
| | **anakumana nawo** | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-024-peter-mother-in-law/ |
| | | **Anthu amene Yesu anakumana nawo - Munthu wakhate** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-025-jesus-leper/ |
| | | **Anthu amene Yesu anakumana nawo - Munthu wosowa thandizo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-jesus-lame-man/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-026-jesus-paralytic/ |
| | | **Anthu amene Yesu anakumana nawo - Mateyu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-027-matthew/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-matthew/ |

| Zoonjezera B - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m'Chithunzi** |
| **B9** | **Mose** | **Kubadwa kwa Mose** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-baby-moses/ |
| | | **Cholakwa chachikulu cha Mose** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-baby-moses/ |
| | | **Mose aona chitsamba chikuyaka moto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-burning-bush/ |
| | | **Mose abweretsa uthenga wa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-burning-bush/ |
| | | |
| **B10** | **Mose** | **Mose ndi mliri woyamba** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-moses-plagues/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/fl-moses-plagues/ |
| | | **Mose ndi mliri womaliza** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/fl-moses-plagues/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-passover/ |
| | | **Mose ndi kuthawa ku Aigupto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-passover/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-red-sea/ |
| | | **Mose ndi Israyeli ayamika Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-red-sea/ |

| Zoonjezera B - Kalasi Yachiwiri Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m'Chithunzi** |
| **B9** | **Mose** | **Kubadwa kwa Mose** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-moses1/ |
| | | **Cholakwa chachikulu cha Mose** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-prince/ |
| | | **Mose aona chitsamba chikuyaka moto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-burning-bush/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-moses2/ |
| | | **Mose abweretsa uthenga wa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-burning-bush/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-moses2/ |
| | | |
| **B10** | **Mose** | **Mose ndi mliri woyamba** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-moses-plagues/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-plagues-1/ |
| | | **Mose ndi mliri wotsiriza** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-plagues-2/ |
| | | **Mose ndi kuthawa ku Aigupto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-moses2/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-red-sea/ |
| | | **Mose ndi Israyeli ayamika Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-food-water/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-moses3/ |

## Zoonjezera B - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B11 | Mose | **Mulungu apereka chakudya** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-moses-manna/ |
| | | **Mulungu apereka chipambano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-amalekites/ |
| | | **Mulungu apereka malamulo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-moses-10-commandments/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-moses-commandments/ |
| | | **Mulungu apereka chipulumutso** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-serpent/ |
| | | |
| B12 | Nkhani ya Khrisimasi | **Yosefe ndi mngelo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/birth-jesus-preschool/ |
| | | **Herode ndi anzeru a kum'mawa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-christmas/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/dm-wise-men/ |
| | | **Anzeru a kum'mawa ndi Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-christmas/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-birth-jesus/ |
| | | **Kuthawira ku Aigupto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-wise-men/ |

## Zoonjezera B - Kalasi Yachiwiri Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B11 | Mose | **Mulungu apereka chakudya** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-food-water/ |
| | | **Mulungu apereka chipambano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-amalekites/ |
| | | **Mulungu apereka malamulo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-sinai/ |
| | | **Mulungu apereka chipulumutso** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-serpent/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-017-nicodemus/ |
| | | |
| B12 | Nkhani ya Khrisimasi | **Yosefe ndi mngelo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/joseph-angel/ |
| | | **Herode ndi anzeru a kum'mawa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-wise-men/ |
| | | **Anzeru a kum'mawa ndi Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-wise-men/ |
| | | **Kuthawira ku Aigupto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-wise-men/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-009-flight-egypt/ |

© Bible Educational Services 2023

www.besweb.com

Registered Charity UK CIO 1186004

NY - 08/2024
(Chichewa)